

Mizimu Yodolola



Mmawa, abwenzi. Wokondwa kuti tiri pano mmawa uno, ndipo podziwa kuti ndakuwonani inu nonse mutatuluka, mukukhulupirira kuti Ambuye ali nafe lero, akutipatsa ife mthunzi wina waung'ono, kuti musakhale motentha kwambiri muno mu kachisi pa msonkhano wa mmawa. Ndipo tsopano ife...

² Ine ndikukhulupirira, kodi pali ana...Kodi ana abalalitsidwa kupita ku makalasi awo, M'bale Neville? Ine ndinawona ana ena aang'ono, ndipo ine ndimangodabwa ngati iwo awabalalitsa makalasi kubwerera kupita ku awo—malo awo ena, kupita ku chipinda chawo cha Sande sukulu.

³ Tsopano, mundipempherere ine. Ine ndiri ndi chiganizo chachikulu chimene ine ndimayenera kupanga usiku watha, ndipo ine ndikuyenera kuchipanga icho lero. Ndipo mpingo upemphere. Ine ndiri—ine ndiri ndi msonkhano umene ukubwera, iwo udzakakhala ku mzere wa Iron Curtain mu Germany, ndipo kotero icho ndi chokhudza pang'ono. Ndipo mundipempherere ine. Ndipo chotero, ndizo, ife tikhoza kudzayamba nthawi yomweyo mu bwalo la kriketi lija mu Germany, limene Hitler analipanga nkondo isanayambike, malo abwino aakulu, mumakhala anthu eyite sauzande. Ndipo ife tikhoza kudzakhala nawo kwa mausiku teni, molumikiza. Ndipo chotero ife tikuyembekeza kuti tikayamba mmenemo nthawi yomweyo, ndipo kenako ku La Salle Lorraine, France, motsatira, kenako ku Berlin, kudzabwerera...ine ndikutanthauza, Berlin pakati pa uko ndi—ndi France.

⁴ Kenako ife tidzabwerera, Ambuye akalola, mu msonkhano waukulu ku Chicago. Udzayamba, ine ndikuganiza, pa faiwi, sikisi, seveni, eyiti, ndi naini, ndi gawo langa mu Chicago, la msonkhano waukulu ku—ku mpingo wa Chiswedish. Ndipo kenako iwo ali, Bambo Boze, ena a inu ochokera ku Chicago, iwo ali ndi msonkhano waukulu umene umabwera motsatira... kuyambira poyambirira pa Ogasti, kapena kumayambiriro kwa Seputembara, izo zidzakakhala, mu Sweden. Ndipo ndine wokondwa kwambiri kudziwa kuti voti yawo kuti ine, kuti ndibwere, ndipo inali ya aliyense ndipo handiredi peresenti. Ine ndinali wokondwa ndi zimenezo, koma ine ndikuyenera mwina kupita kumeneko kapena kumusi kuno tsopano. Inu mupemphere kuti Ambuye anditsogolere ine ndendende basi malo amene miyoyo yochuluka iti idzapulumutsidwe, ndipo zopambana zikachitidwira Ufumu wa Mulungu. Tsopano, iwo ali ndi msonkhano waukulu kumeneko, ndipo—ndipo iwo aku Sweden, ndipo iye anati ife tidzakhala ndi anthu twente-

faivi, sarte-faivi sauzande oti tidzayambe nawo, pa msonkhano waukuluwo, ndipo ambiri a iwo anthu osapulumsidwa.

⁵ Ndipo kenako kumusi kuno mu Germany, chabwino, iwo ali ndi bwalo la masewero limene amakhalamo eyite sauzande. Ndithudi, ife, mu Switzerland kumene ife tangochokako kumene, ife tinali ndi msonkhano wopambana kumeneko, ndipo ambiri a inu mwinamwake simunamvebe. Ambuye anatalitsa ife mwamphamvu, tinali ndi owatembenuza fifite sauzande mu mausiku faivi, ku—ku—ku Zurich, Switzerland.

⁶ Ndipo chotero, M'bale Jack Shuler, ambiri a inu mukumudziwa iye, iye ndi wa Chimethodist, mnyamata wa Bob Shuler wokalamba. Iwo ali ku Belfast tsopano, ndipo—ndipo iwo akuti iwo akungowatembenuza malowo chadodolido, kumeneko, chifukwa cha Uthenga, ndipo ngakhale zazikulu kuposa zimene Billy Graham anali nazo mu msonkhano wake. Jack ndi mnyamata wabwino kwambiri, wodzadza ndi changu ndi chikondi. Ndipo iye—iye ndi woonamtima basi pa izo mpaka ine ndikukhulupirira iye ndi wantchito wopambana wa Ambuye. Ndipo ndikumupempherera M'bale Shuler. Ndipo—ndipo ndi Jack Shuler, ndi Jack MacArthur alinso ndi iwo. M'bale Jack MacArthur ndi mlaliki wopambana, nayenso. Ndipo kumeneko amuna amu mpingo anati icho ndi chitsitsimutso chopambana kwambiri chimene chinayamba chagundapo Ireland. Chotero ndife... Tizipita kukapemphera tsiku lililonse chifukwa cha iwo—amuna amenewo. Iwo awiri onse ndi anyamata, osafika, cha mmaforte, ine ndikuganiza, kapena mmusi, mabanja ndi zina zotero, ndipo aphunzitsi a Uthenga abwino okhazikika, ndipo ife timawakonda iwo.

⁷ Ndipo tsopano, ine—ine ndikupemphera kuti inu musandiiwale ine, kuti—kuti Mulungu andilole ine ndipange chigamulo cholondola pakali pano. Zimakhalapo nthawi zimene sumadziwa kumene ungati utembenukireko. Kodi inu munayamba mwafikapo mmalo amenewo? Ine ndikukhulupirira Paulo anafikapo pa malo amenewo nthawi ina, sichoncho iye? Izo zinali pakati pa makwalala awiri. Ndipo pamene iye anali kudutsa, bwanji, iye anamuwona mngelo mu masomphenya amene anamuza iye, “Bwera ku Macedonia.” Chotero Ambuye adakali nayebe Mngelo Wake apobe, sichoncho Iye? Ngati ine ndingakhale wodzichepetsa basi mu mtima mwanga za izo monga Paulo analiri.

⁸ Ndipo tsopano, usikuuno, mukumbukire misonkhano ya Uthenga kuno ku kachisi, aliyense adzabwere. Inu ozungulira Louisville, ine ndiri woti ndikayankhule ku Church of the Open Door, usikuuno, kwa maora angapo, pa hafu-seveni mpakana hafu-naini, kwa M'bale Cauble. Ine ndinali woti ndibwere kawiri kuno. Ndipo ndiye iye ndi mwamuna wabwino chotero, ndipo iye anandiitana. Ndipo M'bale Cauble, iye ndi mwamuna wabwino kwambiri, m'bale. Inu, ine ndikutsimikiza

inu mukudziwa, m'bale wabwino kwambiri, ndipo basi sindikanamukanira nkomwe iye monga choncho. Pempherani. Pamwamba pa zinthu zonse, pempherani, ndipo mupemphere kuti Mulungu atipatse ife a—chigamulo choyenera choti tichipange.

⁹ Tsopano, ife tisanayambe Ulaliki wa Uthenga, ife tiri ndi mmawa umene ife titi tidalitse ana aang'ono. Ndipo ine ndiri ndi mnyamata wamng'ono apa woti timupereke, nayenso, kwa Ambuye. Tsopano, nthawi zambiri mu mipingo yambiri . . .

Inu mukutha kundimva bwinobwino, kumbuyo uko? Ngati inu mukutero, izo ziri bwino? Zokupizira mphepo izi apa, ine basi, iwe sungathe kudzimva wekha. Ayi, izo, izo ziri bwino. Ine ndikuwopa ine ndingavutike opanda izo.

¹⁰ Chotero a—ana aang'ono, nthawizina iwo amawakonkha iwo, mu tchalitchi, pamene iwo ali makanda aang'ono. Ndipo, ndithudi, zimenezo zinachokera ku mpingo wa Katolika, powabatiza ana aang'onowo, kapena “kuwabatiza” monga iwo amazitchulira izo pamene iwo ali makanda chabe. Mpingo wa Methodisti unazitengera izo, za ubatizo wa makanda, ndi zambiri, ndipo ine ndikuganiza zina zochulukuka. Ine ndikuganiza ndiko kusiyana kwake pakati pa Nazarene ndi a Methodisti akachitidwe kachikale, kunali ubatizo wa makanda, ndipo kenako panali kugawikana pang'ono ndi zina zotero. Koma, njira iliyonseyo, izi sizitero, ine sindikuganiza kuti izo zimakhala ndi vuto kwambiri. Chifukwa, kuwonjezera apo, ine ndikuganiza Kalvare inachotsapo chintchucho, pomwepo, ku zonse za izo, uko nkulondola, chifukwa Yesu anafa pamenepo kuti adzapulumutse ana ndi kupulumutsa dziko.

¹¹ Ndipo mwana wamng'ono, ziribe kanthu kuti ali ndi kholo la mtundu wanji, lochimwa bwanji, zimenezo sizingapange kusiyana kulikonse, pakuti Magazi a Yesu Khristu amamuyeretsa iye, mwaona, ndipo uyu ndi Mwanawankhosa wa Mulungu amene amachotsa tchimo la dziko lapansi. Mwana ameneyo sangathe kulapa. Iye samadziwa momwe angalapire. Iye alibe zifukwa zoti adzakhale kuno, payekha. Iye sangakuuzeni inu chifukwa chimene iye ali kuno. Koma Mulungu anamutumiza iye kuno, ndipo Magazi a Yesu Khristu amamuyeretsa iye mphindi yomweyo imene iye wafika pa dziko lapansi. Ndipo zimakhalapo mpaka iye atafika pa usinkhu wa kuzindikira, ndiye iye amadziwa chabwino ndi choipa, ndipo kenako zimene iye akuchita iye akuyenera kulapa pa zimene iye akudziwa kuti iye akulakwitsa. Uko nkulondola. Chotero, ena a iwo amawakonkha iwo, ndipo amaganiza kuti iwo sapita Kumwamba.

¹² Ndipo pali chiphunzitso chimene chimanena kuti ngati khanda labadwa kwa makolo a Mzimu Woyera, chabwino, mwanayo adzapita Kumwamba; koma, ngati izo si choncho,

palibepo kalikonse kwa iye, mwanayo basi palibepo. Uko ndithudi ndi kulakwitsa. Izo zimapanga kusiyana kwanji ngati iwo ali makolo a Mzimu Woyera? Izo zonse ndi zokhumba za kugonana, ndipo mwanayo amabadwa mwanjira yomweyo. Chotero, izo zonse ndi “kubadwa mu tchimo, kukula mu kusaeruzika, kubwera pa dziko akuyankhula mabodza.” Ndiwo, ndiwo maneno a Malemba a izo.

¹³ Chotero, ndipo kenako Magazi a Yesu Khristu amayeretsa ndipo amapanga chitetezero kwa mwana ameneyo. Ngati iye wafa, iye mwangwiro adzapita molunjika mu Kukhalapo kwa Mulungu, ngati iye anabadwa kuchokera kwa makolo ochimwitsitsa kwambiri mu dziko, mpaka iye atafika zaka za kuzindikira pamene iye akudziwa chabwino ndi choipa. Ndipo kenako zimene iye azichita, kuyambira pamenepo, iye ayenera kuti akhululukidwe chifukwa cha izo. Iye akuyenera kupempha kulapa kwake kwake kuyambira pamenepo mpakana. Koma pamene iye akadali khanda . . .

¹⁴ Tsopano, njira imene ife timayesera kuti tiitsatire, pano pa kachisi. Ndi malo okhawo mdziko amene ine ndimapitako, ine ndimalalikirako Chiphunzitso, ndi kuno ku kachisi, chifukwa ichi ndi tchalitchi chathu. Ndipo ife timalalikira Chiphunzitso kuno kuti tiwayike anthu pa mzere. Anthu ena, mmipingo mwawo, iwo amalalikira chirichonse chimene iwo amakhulupirira. Ndipo iwo ndi abale anga, ndipo ife tikhoza kusiyana pang’ono, koma ife ndi abalebe basi chimodzimidzi. Ndipo, koma kuno mu kachisi, ife timalalikira chimene ife tikuganiza kuti ndi Chiphunzitso cha Mwamalemba. Ndipo, mmenemo, ife timawona kudalitsa kwa ana, chimene ife timachitcha kudalitsa, nthawi yokhayo mu Baibulo imene ife tikhoza kuipeza, kapena pamene mu Chipangano Chatsopano pamene ana anali ndi chirichonse choti achite, kapena Khristu anali ndi chirichonse choti achite mu mwambo umenewo, zinali, Iye anawatengera iwo mmanja Ake ndipo anasanjika manja Ake pa iwo ndipo anawadalitsa iwo, ndipo anati, “Aloleni ana abwere kwa Ine. Musawaletse iwo, pakuti wotere uli Ufumu wa Mulungu.”

¹⁵ Tsopano, ife tinasiidwa, monga ife tikumvetsera, kuti tizipitiriza ntchito imene Iye anabwera kuti—kuti adzaikwaniritse. Imfa Yake pa Kalvare, Iye anali ndi ife ndipo Iye anapita kuchokera . . . anachokera kwa Mulungu, anabwera mdziko, anabwerera kwa Mulungu, kapena kuchokera pa dziko lapansi anapita kwa Mulungu, ndipo anadzabweranso mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, ndipo ali ndi ife, mwa ife, mpaka kumapeto a dziko, akuchita mu Mpingo Wake ntchito yomweyo imene Iye amaichita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Ndipo, ndi zimenezo, ife timawatenga ana athu mmodzi motsatana ndi mzake, kwa atumiki, ndipo iwo amawapempherera iwo, amaika manja awo pa iwo ndi

kuwadalitsira iwo kwa Mulungu. Basi kamwambo kakang'ono konena kuti tikuyamikira chimene Ambuye atichitira ife ndi ana aang'ono.

¹⁶ Tsopano, ngati mwana wanu anakonkhedwa, kapena njira iliyonse imene amachitira ku mpingo wanu, taganizani. Ife sitikunena chinthu chimodzi chotsutsa izo. Izo ziri bwino. Koma, Mwamalemba, ife timangopeza malo amodzi okha, amenewo ndi pamene Yesu anawadalitsa iwo, Iyemwini. Amenewo ine ndiwerenga, Ambuye akalola, mu—mu Mawu apa. Ife tikupeza, mu Luka Woyera a . . . ine ndikukhulupirira ndi mu—mutu wa 10, ndipo kuyambira ndi ndime ya 13.

Ndipo iwo anawabweretsa ana kwa iye, kuti iye awagwire iwo: ndipo ophunzira ake anawadzudzula iwo amene anawabweretsa iwo.

Koma pamene Yesu anawona izo, iye anakhumudwa kwambiri, ndipo anati kwa iwo, Lolani ana adze kwa ine, ndipo musawaletse iwo: pakuti wa oterewa uli ufumu wa Mulungu.

Indetu Ine ndinena kwa inu, Aliyense amene sadzalandira za ufumu wa Mulungu ngati mwana, iye sadzalowa m'menemo.

Ndipo iye anawayangata iwo mmanja mwake, ndipo anayika manja ake pa iwo, ndipo anawadalitsa iwo.

¹⁷ Si zokoma zimenezo? Iye anati, “Tsopano, lolani ana adze kwa Ine. Musawakanize iwo ayi, pakuti wa otere, monga mwana wamng'ono ameneyo, uli Ufumu wa Mulungu.” Ndipo Iye anawatenga iwo mmikono Mwake ndipo anawadalitsa iwo.

¹⁸ Tsopano, mmene ife tingakondere, mmawa uno, ngati ife tikanakhala ndi Yesu atakhala, ngati munthu, pano pa nsanja, ndikuti, “Ambuye, kodi Inu mungamudalitse mwana wanga?” Oh, izo a . . . pakuti maso athu a umunthu ndi mitima yathu ikufuna kuwona izo. Koma Iye ali pano, mulimonse, pakuti Iye anatipatsa ife ulamuliro wochita izo. Ndipo, monga ife tachitira, chomwechonso Iye amachizindikira. Ife timalandira amene Iye anawatumiza, kumulandira Iye amene anamutumiza iye, inu mwaona. Chotero, Iye ali pano mmawa uno. Ndipo ngati Mlongo Gertie angabwere pa limba ndi kudzaimba nyimbo yathu yakale imene ife tinkakonda kuimba kalekale, iyi, “Abweretseni iwo, abweretseni anawo kwa Yesu.” Ine ndikukhulupirira iyo ili mu bukhu mmenemo penapake. Ine sindikutsimikiza. “Abweretseni anawo kwa Yesu.” Ndipo ngati inu muli ndi mwana, khanda amene sanadalitsidwe, ndipo inu mukufuna kuti mumudalitsitse iye mmawa uno, bwanji, ife tikhala okondwa kuchita zimenezo.

¹⁹ Ndipo kodi alipo atumiki aliwonse mchipinda chino, alaliki amene angafune kubwera ndi kudzaima ndi ife pano pamene ife tikuwadalitsitsa ana awa kwa Ambuye? Ife tikhala okondwa kukhala nanu, pamene inu mukubwera. Chabwino, kodi iyo

ilimo m'bukhu mmenemo? Inu mwayipeza iyo, M'bale Neville? Iyo mulibemo mmenemo. Chabwino, ndi angati amaidziwa iyo, *Abweretseni Iwo?* Chabwino, tiyeni tiyimbe iyo tsopano. Aliyense pamodzi, pamene amayi akubweretsa ana awo. Chabwino. Chabwino.

. . . iwo mkati, abweretseni iwo mkati,
Abweretseni kuchokera ku minda ya tchimo;
Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni oyendayendawo kwa Yesu.

Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni iwo kuchokera ku minda ya
tchimo;
Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni aang'onowo kwa Yesu.

²⁰ Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa mphindi. Atate athu Akumwamba, ayima mozungulira guwa mmawa uno ndi amayi ndi abambo atanyamula mphukira zawo zazing'ono mmikono mwawo, amene Inu mwachisomo mwazipereka kwa iwo. Iwo ndi othokoza kwambiri chifukwa cha izo, Ambuye, ndipo iwo akuwabweretsa iwo pano pa guwa mmawa uno, mnyumba ya Mulungu, kuti awadalitsitse iwo, kudzapereka miyoyo yawo kwa Inu. Inu mwapereka. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwasamalire ndi kudalitsa mmodzi aliyense wa iwo. Atsogolereni iwo, ndipo mulole Angelo olondera a Mulungu ayang'anire mmodzi aliyense. Apatseni iwo miyoyo yaitali ya chisangalalo ndi chimwemwe. Mulole iwo adzawuke kukhala amuna ndi akazi a Mulungu, a mawa, ngati mawa alipo.

²¹ Mulungu, ife tikupemphera kuti Inu mudzadzutse alaliki ndi aneneri ndi aphunzitsi kuchokera mwa gulu ili la ana limene liri mozungulira guwa ili mmawa uno. Ndipo pamene ife tidzakalambe ndipo nkusatha kupitirira patsogolo, winawake nkumachita kutitenga ife kuchoka pa malo kupita pa malo, mulole ife tidzakwanitse kuyima ndi kumva Uthenga ukulalikidwa ndi awa amene ali pano lero. Perekani izi, Ambuye. Ndipo tsiku lina la ulemelero pamene zonse zidzatha, miyoyo yathu itatha, makolo awa atazungulira guwa, mulole ife tidzakhale ngati Yakobo wakale pamene iye ankawadalitsa ana ake onse ndipo anawauza iwo chimene mathero awo ati adzakhale mu tsiku lotsiriza. Kenako poyang'ana mmwamba, anati, "Inu mukudziwa, ine ndikuyenera kudzasonkhana ndi anthu anga." Ndipo tsiku lina la ulemelero, iye ndi mphukira zake zonse, adzakasonkhane pamodzi mu dziko labwinoko. Nzosadabwitsa Balamu anati, "Mulole mapeto anga otsiriza adzakhale ngati ake." Mulungu, ine ndikupemphera kuti Inu mudzapereke madalitso awa pa makolowo.

²² Ndipo tsopano pamene ife tikupita kukayika manja pa iwo, ndi—ndi chopambana bwanji. . . Ndipo ndi modzichepetsa

bwanji mmene Inu mwazipangira izo, Ambuye, kuti ife anthu a pa dziko lapansi lino tingakhale ndi mwayi wodalisita ana aang'ono mu Dzina Lanu, podziwa ichi, kuti, chimene ife tachipempha, ife tapatsidwa. Pamene ife tikupita kukawadalitsa iwo, mulole Yesu, Munthu wosawonekayo, wamphamvuzonse Uyo ayime pafupi ndi kudalitsa mwana aliyense pamene ife tikuyika manja athu pa iwo ndi kuwapereka iwo kwa Iye. pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Ameni.

²³ M'bale Glenn Funk, iye ali ndi ana ake atatu oti aperekedwe kwa Ambuye.

[Malo opanda kanthu pa tepi. M'bale Branham akuwadalisita ana—Mkonzi].

...a—mkachipinda kakang'ono, kutali uko mu dziko la kumpoto, Inu munalonjeza mwana uyu kwa ine. Atate, mulole madalitsa Anu akhale pa iye.

Joseph, mwana wanga, ine ndikukupereka iwe kwa Mulungu. Ndipo moyo wako ukhale mdalitsa. Iwe udzakhale mneneri, Joseph. Chisomo cha Mulungu chizikhala ndi iwe. Mulungu wa atate ako, Ambuye Yesu Khristu, nthawizonse azikudalitsa iwe, apange moyo wako kukhala mdalitsa kwa ena.

Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikumudalitsa iye. Ameni.

[Malo osajambulidwa pa tepi. M'bale Branham akudalitsa ana—Mkonzi].

²⁴ Mumakonda ana aang'ono? Chinachake chokhudza ana kuti mayi aliyense amafuna mwana wake kuti adalitsidwe.

Tsopano, umo ndi mmene Atate athu Akumwamba aliri kwa ife akulu akulu mmawa uno. Iye akufuna aliyense wa ife kuti tidalitsidwe. Iye amatipereka ife patsogolo pa chinthu chinachake, amangochipereka icho kwa ife, monga kunena kuti, “Apa, ine ndikufuna iwe udalitsidwe, mwana Wanga.” Kodi Iye si wodabwitsa? Chotero ife tikhoza kuyamikira mtundu wa Atate Akumwamba ngati amenewo.

²⁵ Tsopano, mu kudalitsa ana aang'ono, inu mukudziwa, ine ndimangowerenga apa mu Lemba tsiku lina, penapake apa, iwo anali mu Chipangano Chakale, kuti, chinthu chachikulu chimene ine—ine ndithudi ndinayamikira kuchiwerenga. Ndi ichi apa, pomwe apa. “Ndipo Nataniele anati kwa Davide, ‘Uchite zonse zimene ziri mumtima mwako, pakuti Mulungu ali ndi iwe.’” Mukuona? Uchite chimene chiri mu mtima mwako. Ndipo nthawi zambiri ine—ine ndachipeza ichi, mzanga wa Chikhristu, kuti ine ndayankhulapo zinthu osadziwa chimene ine nditayankhule, ndipo nkudzapeza kuti chachitika. Chimene iwe unanena!

²⁶ Zinanenedwapo nthawi ina, Yesu anatsika kuchokera ku phiri ndipo Iye anawuwona mtengo umene unalibe kalikonse mwa iwo, unangotsala ndi masamba basi, ndipo munalibemo

chipatso, ndipo Iye anati, “Palibe munthu adzadye kuchokera mwa iwe kuyambira pano.”

²⁷ Ndipo tsiku lotsatira, akudutsa, atumwi anawona masamba atanyala. Iye anati, “Taonani mmene mtengowo wanyalira mwachangu.”

²⁸ Yesu anati, “Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu; pakuti chinthu chirichonse inu muchikhumba, pamene inu mupemphera, khulupirirani mulandira icho ndipo inu mudzakhala nacho icho. Ndipo chinthu chirichonse inu munganene, inu mudzalandira chimene inu mwanena.” Taganizani za zimenezo. Oh! Ndipo mwinamwake lero, Mzimu Woyera waukulu wa Mulungu, wayima pano pa guwa, inu mukuti... Chabwino, ilo silikuyenera kukongoletsedwa. Ilo silikuyenera kukhala malo ena apamwamba.

²⁹ Yakobo anakoka mwala nthawi ina ndipo anagonetsa mutu wake pa iwo, ndipo iwo amazindikiridwabe lero ngati Stone of Scone. Kapena, Mwala Wosongoka, kuti amuna aakulu a dziko lapansi amasonkhana mozungulira mwala umenewo, kuti mafumu adzozedwe pamwamba pa mwala uwu, basi mwala wamba wakale utakhala mmunda.

Bethel anangokhala mulu wa miyala itaikidwa pamwamba pa imzake, ndipo iyo inadzakhala nyumba ya Mulungu, malo okhalamo. Yakobo anati, “Awa si malo ena koma nyumba ya Mulungu.” Basi mulu wa miyala ili pamwamba pa wina ndi imzake.

³⁰ Izo sizitengera zinthu zazikulu zapamwamba. Izo zimatengera kuphweka ndi chikhulupiriro kuti ukhulupirire, ndi zomwe zimatengera. Ndi zomwe zimapanga izo.

³¹ Tsopano, podziwa kuti nthawi itha pompano, ife tiyesera kuti tisakusungeni inu motalika kwambiri, podziwa kuti kwatentha ndipo tchalitchi chadzaza. Chotero ine ndingoyankhula ndi inu mphindi pang’ono chabe mmawa uno, pa phunziro laling’ono apa limene mwinamwake... ine ndikudalira ilo likhala thandizo kwa inu. Ndipo tsopano ine, ndisanapite kwathu, ine ndinalemba zinthu zazing’ono zitatatu kapena zinai. Ine ndinati, “Ine ndidikirira ndi kuwona chimene Ambuye angafune kuti ine ndiyankhulepo pamene ine ndikafika kumusi kumeneko.” Ine ndinalemba pafupifupi zinthu sikisi zazing’ono kumusi kuno, maphunziro pang’ono, ndipo ine ndinalemba limodzi, ndinayika ilo mthumba mwanga monga chonchi. Ine ndinaganiza, “Chabwino, pamene ine ndikafika paguwa mwinamwake Iye akandiuza ine chinachake choti ndiyankhulepo.” Tsopano ine ndiri basi patali monga ine ndinaliri kumtunda uko. Chotero, mulimonse, ine ndiwerenga Lemba apa, Ambuye atithandize ife kuti tiwamvetse Iwo. Mutu wa 14 wa Luka Woyera, ndipo tiyeni tiyambire pa sarte... ndime ya 31 ya mutu wa 14 wa Luka Woyera.

Kapena mfumu yotani, ikupita kuti akamenye nkhoondo ndi mfumu ina, simakhala pansu poyamba, ndi kufunsira ngati iye ali wothekera ndi teni sauzande woti akakumane ndi iye amene akubwera motsutsana naye ali ndi twente sauzande?

Kapena mwina, pamene iye ali mwina... iye akadali kutali, iye amatumiza patsogolo wokazonda, ndipo amafuna migwirizano ya mtendere.

Chotero chimodzimodzi, aliyense iye angakhale wa inu...

³² Ine ndikufuna inu muzindikire mwatcheru. Tsopano, poyamba Iye anati... Ilo ndi fanizo. Iye anati, "Tsopano, pali mfumu ikubwera, ndipo iyo ili ndi asirikali twente sauzande; ndipo mfumu *iyi* ikukakumana naye iye, ndipo iye ali ndi asirikali teni sauzande okha. Chotero ndiye, poyamba, iye amakhala pansu ndi kufunsa ngati iye wakonzeka, ngati iye angachite izo kapena ayi." Chabwino.

... a inu amene simusiya zonse zimene iye ali nazo, iye sangakhale wophunzira wanga. (Mukuona?)

³³ Tsopano Ambuye awonjezere mdalitso Wake ku Mawu awa. Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

³⁴ Atate athu Akumwamba, Inu Amene mumadziwa zinthu zonse, ndipo simumalabadira umunthu wa munthu, pakuti munthu ndi ndani kuti Inu mumamuganizira iye? Inu munamupanga munthu, ndipo iye basi ali ngati duwa la mmunda: lero ndi wokongola, mawa wadulidwapo, nkuponyedwa mu uvuni, ndipo iye nkunyalapo. Ndipo ine ndikukupemphani Inu, Mulungu, kuti mutichitire ife chifundo lero ndipo mulole aliyense adzifufuze lero. Ife tiri pano ngati mnyumba yokonzedweramo. Ife tiri pano kuti tidzaphunzire ndi kudziwa mmene tingakhaliro moyo, ndipo mulole izo zichokere ku Mawu Anu lero, O Mulungu Wamuyaya. Ambiri a ana Anu asonkhana, ndipo ambiri a iwo akhala ali ana Anu kwa zaka, koma, monga choncho, ife tonse tikubwerera ku nyumba ya Mulungu, kuti tidzaphunzire, kuti tidzadziwe. Ndipo ine, wantchito Wanu, ndikukhumba kudziwa zochuluka za Inu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mubweretse kudzoza kwa Uthenga pa ife tonse, pa wantchito Wanu, ndipo kuti Kukhalapo Kwanu, ndi kutidzoza ife kudutsa mchipindachi, kukhale kwakukulu lero, kuti ife tizichoka, mu mtima mwathu, tikukhumba kukhala antchito Anu abwinoko, kuti izo zikhale zopindulitsa kwa ife kukhala pano. O Mulungu wachifundo, perekani madalitso awa mu Dzina la Yesu, Mwana Wanu. Amen.

³⁵ Tsopano Ambuye awonjezere madalitso Ake ku Mawu pamene ife tikuwerenga. Ine ndikufuna kuti nditenge phunziro mmawa uno, lakuti, "Mizimu yodolola kapena Mawu a

Mulungu?” Tsopano, wokhala ngati mutu wachirendo, koma pokhala kuti izo ziri mu kachisi...Ndipo Lachitatu lapitali usiku...Lamlungu lapitali mmawa ine ndimayankhula pa—chikondwerero chaching’ono cha Uthenga.

³⁶ Ndipo usiku wa Lachitatu lapitali ine ndimalalikira za mkazi amene anali ndi—chigwinjiri pamutu pake, kapena a...Iye anataya chidutswa chimodzi cha zigwinjiri zake, ndipo iye anali kusesa mnyumba ndi kumayesera kuti achipeze icho mwamuna wake asanabwere. Ndipo tinadzapeza kuti mkazi ameneyo anali mkazi wa kummawa, ndipo iye...ndipo amaimirira Mpingo. Ndipo mphete ya ukwati sinkavalidwa pa chala. Iyo inkavalidwa mozungulira mutu, ili ndi zidutswa naini za siliva pa iyo. Ndipo pamene mkazi akhala wachiwerewere, iwo ankachotsa chidutswa chimodzi cha siliva ndipo zinkawonetsera kuti iye anali wachiwerewere. Ndipo chotero mkazi uyu anali atataya chimodzi cha zidutswazo, sanali wachiwerewere. Koma mwamuna wake anali atachoka, ndipo iye anali kuyesetsa kufulumira kuti apez chidutswa chimenecho, kuti achibwezeretse icho mu tabuleti yake, pakuti mwamuna wake akabwera iye adzadziwa kuti iye anali atagwidwa mu chiwerewere, ndipo izo zikanatanthauza kuphwasuka kwa nyumba ndi zina zotero. Ndipo ine ndinafanizitsa izo kwa mphindi zochepa ku mpingo, unataya zinthu zazikulu zambiri. Ndipo ndi nthawi yoti Atate abwere, chotero ife tikuyenera kuzifunafuna izo. Tsopano, podziwa mu tchalitchi, ndipo kachisi wathu. . .

³⁷ Ndipo ine—ine ndikufuna ndiyankhule pa *Mizimu Yodolola*, zimene kwenikweni mutu wake ndi *Phunziro la ziwanda*. Inu mumamva zochuluka za ziwanda, za masiku ano, koma inu mumamva zochepa za mmene mungazichotsere izo. Ife tonse—timadziwa bwino kuti kuli ziwanda, koma, chinthu chotsatira ndi, mmene mungachichotsere chinthu chimenecho. Ndipo tsopano pali...Kukhala, mwa chisomo cha Mulungu, mwayi wochuluka wochita ndi zinthu izi zotchedwa ziwanda, ndi kukumana nazo pa guwa ndi kuyenda kwa tsiku ndi tsiku, ndipo, bwanji, ine ndikufuna ndiwone mu Lembu mmawa uno ndi kupeza basi chimene zinthu zimenezo ziri.

³⁸ Tsopano, ife taziika izo mu msonkhano wa machiritso, nthawizonse mbali ya machiritso. Khansa, chotupa, ng’ala, chifuwa chachikulu, zinthu zonsezo si zinthu zachirengedwe, izo ndi zauzimu ndipo ndi ziwanda. Malemba poyera amatsimikizira izo. Koma zimenezo ndi ziwanda mu thupi, ziri ndi zophuka, ngati khansa, ziri ndi moyo mkati mwake, ndipo moyo wa izo ndi chiwanda. Chotupa cha ng’ala, kufala kwa chifuwa chachikulu, ndi matenda ena, ndi ziwanda. Izo ziri m’kawonekedwe kuthupi.

³⁹ Tsopano, mmawa uno ife tiyankhula—tiyankhula za ziwanda mu kawonekedwe auzimu mu solo. Izo ziri mu

solo chimodzimodzi monga ziri mu thupi. Ndipo ife ndi okakamizidwa kuvomereza kuti ife timaziwona izo mu thupi la munthu, monga khansa ndi—ndi matenda amene ali mu thupi la munthu.

⁴⁰ Chapompano, ngakhale khansa yanenedwa kuti ndi nthenda ya mdera lachinayi, kuti iyo ili mu dera lina. Ndithudi, ndi zokhudza ziwanda. Nthenda iliyonse ndi nthenda ya dera lachinayi, chiyambi chake.

⁴¹ Tsopano, koma tsopano khansa mu thupi kapena khansa mu solo, chiwanda chikhoza kubwera pa malo aliwonse. Tsopano, pali nthawi zambiri ndi anthu ambiri a malingaliro abwino amene. . . ndipo anthu abwino amene amayesetsa nthawi zambiri ku—kukhala pa fioloje yina imene iwo ali nayo, kapena chinachake chimene iwo anaphunzitsidwa kuyambira ali mwana, ndipo amachipezabe pansu pa umunthu wawo, pansu mu solo yawo, kuti iwo ali ndi chinachake chimene sichoyenera. Inu, ambiri ali pano mmawa uno, nzosakaikitsa kulikonse kumene mumapeza Akhristu atasonkhana pamodzi, inu mumapeza anthu amene ali ndi mizimu imeneyo mwa iwo, kuti iwo. . . Izo ndi zosakhumbika. Iwo samazifuna izo. Iwo amati, “Oh, ngati ine ndingasiye kunama! Ngati ine ndingasiye kusirira! Ngati ine ndingasiye *ichi* kapena *icho!*” Tsopano, izo ndi ziwanda. Ndipo, tsopano, iwo amabwera mu mawonekedwe a chipembedzo, nthawi zambiri. (Pokhala kuti ndi Sande sukulu, ndi nthawi yophunzitsa, chotero tiyeni tiwone ichi.) Tsopano, iwo amabwera mu mawonekedwe a chipembedzo, nthawi zambiri.

⁴² Tsopano, mu Lemba, kamodzi, panali munthu dzina lake Yehosafati, mwamuna wamkulu, munthu wachipembedzo. Ndipo iye anapita kwa mfumu wina amene anali mfumu ya—ya Israeli. Ndipo iye, Yehosafati, anali mfumu ya Yuda. Ndipo iye anapita kumusi kwa Ahabu, mfumu ya Israeli, ndipo iwo anazilumikiza pamodzi, ndipo anapanga mgwirizano ndi wina ndi mzake, kuti apite kukamenya ku Ramoth Gileadi. Ndipo iwo anapanga izo opanda kuyamba apemphera kaye.

⁴³ Oh, ngati anthu angazindikire! Ndi chifukwa chimene ine ndabwera mmawa uno ndi kukufunsani inu kuti mundikumbukire ine pamene ine ndikupita kutsidya kwa nyanja. Mu zinthu zonse, pempherani!

Winawake anabwera tsiku lina ndipo anati, “M’bale Branham, kodi inu mukuganiza ndi cholakwika kupanga chinthu chinachake?”

⁴⁴ Ine ndinati, “Iwe ukufunsa za chiyani?” Mukuona? Ngati pali funso mmalingaliro mwanu, zisiyeni izo, musazichite konse zimenezo. Mungokhala ndi ilo. Pamene inu muyamba kupanga chirichonse, ndipo ngati pali funso kuti mwina ndi cholondola kapena ayi, talikiranani ndi izo. Musalowe konse mu zimenezo, kenako inu mumadziwa kuti mukulondola.

⁴⁵ Tsopano, zinthu zonse zikuyenera kuganiziridwa mwapemphero, poyamba. “Yambani mwathanga Ufumu wa Mulungu ndi chirungamo Chake, ndipo zinthu zina zonsezi zidzawonjezedwa.” Ndine wotsimikiza ndithudi mmawa uno, ngati amuna ndi akazi angafike pamalo amene solo yawo, kuganiza kwawo, khalidwe lawo, lingakhale langwiro pamaso pa Mulungu, umenewo ungakhale umodzi wa mipingo yamphamvu umene unayamba wakhalapo.

⁴⁶ Onani mphindi zochepa pa zakuthupi. Tsopano, ife, tiri, nthawi zambiri, kwa zaka, ife tiri ndi chimene timachitcha “chozindikira bodza.” Inu mukhoza kuchiika icho pa nkono wanu, kuchiika icho pa wawo—mutu wawo, ndipo inu mukhoza kulowa mmenemo ndi kuyesera mopambana momwe inu mungathere kuti mulipange bodza limveke ngati choonadi, ndipo icho chiwonetsera kulakwitsa nthawi zonse, chifukwa munthu sanapangidwe kuti azinama. Kunama ndi chinthu chonyenga, chovuta, chinthu choipa. Ine ndingakonde nditakhala ndi woledzera ndi ine, tsiku lililonse, kusiyana ndi wabodza. Mukuona? Wonama! Ndipo thupi lanu silinapangidwe kuti lizinama. Ziribe kanthu mmene iwe uliri wochimwa, iwe ukadali mwana wakugwa wa Mulungu. Munthu wochimwitsitsa mu mzinda uno lero, Mulungu sanakupange iwe kuti ukhale wochimwa. Iye ankafuna iwe ukhale mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Iye. Iwe unapangidwa mu mapangidwe a Iye Mwini. Koma tchimo lakupangitsani inu kuti muzichita zimenezo. Ndipo ziribe kanthu mmene iwe ungayesere kunyengezera ndi kuyesera kulipanga bodza kukhala lowona, iwo ali ndi chida cha sayansi chimene chimatsimikizira kuti ndi zolakwika. Iwe ukhoza kunena izo ndi kuwona mtima konse kumene iwe ukukufuna, koma icho chimakanabe; chifukwa pali chikumbumtima pansu mwa munthu, ndipo chikumbumtima chimenecho chimadziwa chimene chiri cholondola. Ndipo ziribe kanthu chimene inu mukunena kunja kuno, chikumbumtima chimenecho chimadziwa kuti ilo ndi bodza, ndipo chisemphana ndi chikumbumtima.

⁴⁷ Chotero, ngati mwamuna kapena mkazi angatenge malingaliro awo, ndipo umboni wawo ndi miyoyo yawo italumikizana ndi Mulungu (ameni) mpaka mpita wa Mzimu Woyera nkukhala umodzi mwangwiro ndi Mulungu, chingachitike nchiyani! Ngati mwamunayo ndi mkazi angafike polumikizana, pamene ndi ufulu kuchokera mumtima mwawo, ndi chikhulupiriro chochokera mkatikati!

⁴⁸ Anthu ambiri amabwera paguwa kuti adzapemphereredwe, iwo amakhala ndi chikhulupiriro cha luntha. Iwo amavomereza machimo awo ndi kujowina mpingo, mwa chikhulupiriro chaluntha. Iwo amakhulupirira izo mu awo—mmalingaliro awo. Iwo amakhulupirira izo chifukwa iwo azimva izo. Iwo amakhulupirira izo chifukwa iwo amadziwa kuti ndi mfundo

yopambana. Koma icho si chimene Mulungu amachiyang'ana. Iye samayang'ana pa chikhulupiriro chako cha luntha.

⁴⁹ Iye amayang'ana mu mtima, kumene mkati Mulungu. . . Ndipo pamene izo zichokera mu mtima, zinthu zonse zimakhala zotheka ndiye. Kuvomereza kwanu kumakumana ndi moyo wanu. Moyo wanu umayankhula mofuula monga momwe kuvomereza kwanu kumachitira.

⁵⁰ Koma pamene kuvomereza kwanu kunena chinthu chimodzi, ndipo moyo wanu nkumakhala chinthu china, pali chinachake cholakwika penapake. Icho ndi chifukwa choti muli ndi chikhulupiriro cha luntha, ndipo osati chikhulupiriro chochokera mu mtima mwanu. Ndipo izo zimawonetsera kuti kunja, *uku*, kuli chidziwitso cha Mulungu; koma mkati, *umu*, ndi chiwanda chikukaikira. “Ine ndimakhulupirira mu machiritso Auzimu, koma iwo si anga.” Mukuona? “Ah, izo zikhoza kukhala chomwecho, koma ine sindikhulupirira zimenezo.” Mukumvetsa zimenezo? Kunja, inu mukuti “inde”; mkati, chikumbumtima chanu chimati “ayi.” Chinthu cha sayansi chomwecho chimatsimikizira kuti izo sizinali zolondola, chimatsimikizira izo.

⁵¹ Tazindikirani pamene mafumu awa, iwo asanayambe, iwo amayenera kukhala. . . Yehosafati asanapange mgwirizano ndi Ahabu, iye ankayenera kunena poyamba, “Tiyeni tipemphere ndipo tiwone chimene chiri chifuniro cha Ambuye.”

⁵² Ndipatseni ine mlaliki, ndipatseni ine Mkhristu, ndipatseni ine mkazi wapanyumba amene ali Mkhristu, ndipatseni ine mlimi, kapena wantchito waku fakitore, amene angamuyike Mulungu poyambirira mu chirichonse, ine ndikuwonetsani inu munthu amene angachite bwino posawerengera zoipa zonse zimene zingaidwe pa iye. Iye amamufunafuna Mulungu, poyamba. Iye tikuyenera poyamba kukhala. . .

⁵³ Koma iwo sanachite zimenezo. Iwo onse anaunjikana chifukwa Ahabu anali ndi ufumu waukulu wowala, ndipo iye anali atachita zinthu zambiri, ndipo anali ndi zipala zazikulu, golide wake ndi siliva wake, anali wopambana, mwamuna wochita bwino, komabe wosakhulupirira.

⁵⁴ Ndipo pamenepo ndi pamene dziko liri lero. Pamenepo ndi pamene mipingo yayima lero. Iye tamanga mipingo yapamwamba imene inayamba yamangidwapo. Iye takhalapo nawo ena a masikolala opolishidwa amene tinayamba takhalapo nawo. Iye taphunzitsapo fioloje yapamwamba, ndi zina zotero, ndipo taphunzira kuyimba ngati Angelo, komabe pali chofooka penapake. Pali kufooka, chifukwa iwo atsatira chiphunzitsa cha munthu ndi mizimu yodolola, mmalo mobwerera ku Mawu a Mulungu. Iwo amayesera kupanga zinthu kuti zifanane ndi

dziko. Iwo ayesera kuyika kuwala konyezimira pa izo, ngati Hollywood.

⁵⁵ Kuno tsiku lina, chipembedzo chotchuka, gawo la Full Gospel mu Kansas City, kapena, mundikhululukire ine, ku Denver, pa msonkhano waukulu, akumanga tchalitchi cha madola milioni. Ndipo masauzande amamishonare akudikirira masenti fifite kuchokera ku chipembedzo chomwecho, kuti anyamule Uthenga kupita nawo kwa achikunja. Chimene ife tikuchisowa lero ndi chitsitsimutso cha malingaliro a umishonare, chotumizidwa ndi Mulungu, chobadwa ndi Mzimu Woyera, chimene chitakhale ndi chikoka cha Mulungu, kuti chikankhire kunja kulowa ku nkhalango uko ndi kukamuchitira chinachake Mulungu, mmalo momanga mipingo yaikulu, yabwino ndi kumayesera kumuposa woyandikana naye.

⁵⁶ Ine ndingakonde kuti ndizipembedza mu mishoni, kumene kunasesedwa, kapena ku bala, ndi kukhala ndi mtendere wa Mzimu Woyera ndi chikondi cha Mulungu chikutentha mmitima, kusiyana ndi kukhala mu kachisi wamkulu amene ife tiri naye mdziko ndi kumangiridwa pansu ndi ziphunzitso ndi nthano za munthu. Ife tikusowa lero chitsitsimutso chogwedeza, kubwerera ku Choonadi, kubwerera ku Mawu a Mulungu kenanso.

⁵⁷ Tsopano, pamene iwo anapita kunja kumeneko, ndipo izo zinali patapita nthawi Yehosafati anakhala ngati wadzikumbukira iyemwini ndipo anati, “Kodi... Chabwino, tiyeni tiwafunse Ambuye za ichi.”

⁵⁸ Iye anati, “Chabwino,” Ahabu anatero, ndipo iye anapita kumusi ndipo anapeza handiredi, alaliki ophunzitsidwa bwino foro handiredi. Ndipo iye anawabweretsa iwo kumeneko ndipo anati, “Onsewa ndi aneneri.”

⁵⁹ Ndipo chotero iwo anapita mu zowombeza zawo, ndipo iwo anayamba kuyitana. Ndipo iwo anati, “Inde, inu mukhoza kupita mu mtendere. Ambuye ali ndi inu.”

⁶⁰ Ndipo kenako foro handiredi onsewo atachitira umboni kuti iwo apite mu mtendere, komabe Yehosafati podziwa... Inu mukumvetsa zimenezo? Mwaona, pansu mu mtima wa munthu woyera ameneyo munali chinachake chimene chinamuza iye kuti panali chisoso mu nsuzi penapake. Chinachake chinalakwika.

⁶¹ Ahabu anati, “Tsopano ife tiri ndi foro handiredi apa, ndipo mu mgwirizano umodzi, aliyense wa iwo akuti, ‘Pitani, Ambuye ali ndi inu.’”

Koma Yehosafati anati, “Kodi inu mulibe mmodzi wina?”

⁶² Iye anati, “Chabwino, ife tikufuniranji mmodzi wina, ife titapeza foro handiredi a amuna ophunzira apamwamba mdziko? Iwo onse akuti ‘Pitani!’” Izo zinali za luntha. Koma

pansi mu mtima mwa Yehosafati iye anadziwa kuti panali chinachake cholakwika. Tsopano, iye anati, “Ife tiri naye mmodzi wina, iye ndi Mikaya. Koma ine ndimadana naye iye.” Anati, “Iye nthawizonse amanena chinachake choipa, ndipo amatulukira pamene alibe choti achitepo, ndipo iye akuchepsya mipingo ndi chirichonse.” Anati, “Ine ndimamuda iye.”

Anati, “Pitani, kamutengeni, ndipo tiwone chimene iye ati anene.”

⁶³ Ndipo pamene Mikaya anabwera, iye anati. . . Iwo anati, “Tsopano, ona, iwe unene chinthu chomwecho monga ena onsewo.”

⁶⁴ Iye anati, iye anati, “Ine basi. . .” Ndi izi apa. “Ine ndinena chimene Mulungu atanene.” Ameni. “Ziribe kanthu chimene mneneri wanu wanena, ndi chimene *uyu* akunena, ndi chimene mpingo wanu ukunena, ndi chimene iwo akunena. Ine ndinena chimene Mulungu akunena. Mulungu ayika pa milomo yanga ndipo ine ndinena chimene Iye akunena.” Chimene ife tikuchisowa ndi a Mikaya ambiri amene adzinena chimene Mulungu wanena. Zindikirani, chotero iwo anamubweretsa iye kumeneko, ndipo iye anati, “Ndi patseni ine usikuuno.” Chotero usiku umenewo Ambuye anakumana ndi iye, ndipo iye anabwerera mmawa wotsatira. Pamene mafumu awiriwo anakhala pa chipata, iye anati, “Kwerani kumeneko.” Anati, “Kwerani kumeneko. Koma,” anati, “Ine ndinawona Israeli ali ngati nkhosa zomwazikana zopanda m’busa.”

⁶⁵ Chotero mlaliki mmodzi uyu, atavala bwino, anayenda ndipo anamumenya iye pakamwa, ndipo anati, “Mzimu wa Mulungu unapita njira iti pamene Iwo unachoka kwa ine?”

Anati, “Iwe uzindikira ukamabwerera.” Inde.

⁶⁶ Iye anati, “Tamverani apa!” Iye anati, “Ife ndi antchito a Mulungu. Ife tiripo foro handiredi, ndipo iwe ulipo mmodzi.”

⁶⁷ Koma Mikaya anati, “Ine ndikuuzani inu pamene vuto lanu liri.” Ameni! Anati, “Ine ndinawona masomphenya.” Ameni! Iye anati, “Ndipo ine ndinawona Mulungu atakhala pa mpando Wake wachifumu. Ine ndinawona khamu la Kumwamba litaima momuzungulira Iye. Ndipo ife tikudziwa kuti Mawu a Mulungu ayankhula matemberero pa munthu uyu, chifukwa cha mmene iye wachitira.”

⁶⁸ Iwe sungadalitse chimene Mulungu wachitemberera, komanso mdierekezi sangatemberere chimene Mulungu wachidalitsa. Icho ndi chokuchitikira cha pawekha, ziribe kanthu kaya ndiwe wosauka chotani kapena wopusa chotani, mmene uliri wosaphunzira, wopanda maphunziro. Chimene Mulungu wachidalitsa ndi chodalitsidwa. Chimene Mulungu wachitemberera ndi chotembereredwa. Muzidziwa kusiyanita chabwino ndi choipa.

⁶⁹ Mikaya anadziwa bwino ndi moona kuti ameneyo sanali Ambuye amene anali ndi alaliki amenewo. Chabwino, vuto linali chiyani ndi alaliki amenewo? Zindikirani chimene iwo anachita. Iwo anali atavala zapamwamba. Iwo anali atadyetsedwa zapamwamba. Iwo anali atabwera pamodzi mu maphwando awo ndi zina zotero, ndi migwirizano yawo, mpaka malowo anafika poti iwo ankangodziwa fioloje yawo. Ndipo Baibulo linanena kuti Mikaya, pamene iye anali kuyang'ana pa masomphenyawo, iye anati, "Mulungu anati, 'Ife timutume ndani kuti apite uko ndi kukamunyenga Ahabu?' Ndipo mzimu wabodza unati, 'Ine ndipita pansi pamenepo ndipo ndikamukopa Ahabu kudzera mwa alaliki amenewo, kuti ndikamupangitse Ahabu kupita kunja kumeneko, kuti Mawu a Mulungu akakwaniritsidwe.'"

⁷⁰ Tsopano, lero anthu ambiri akumvetsera... (Tsopano, Sande sukulu, ine ndimaikonda iyo.) Taonani, anthu ambiri amamvetsera mizimu yodolola mmalo motenga Mawu a Mulungu. Mizimu, iyo ilipo mdziko. Iyo ndi ziwanda. Ndipo iyo imapita mmalo ndipo iyo imafika pakati pa anthu, atumiki. Iyo imafika pakati pa mamembala a mpingo. Iyo imafika pakati pa anthu abwino. Ndipo iyo imawapangitsa iwo kuti abwere mu, kubalalika. Ndipo iwo amanena zinthu, ndipo amachita zinthu, ndipo amaphunzitsa zinthu, ndi kumapanga zinthu, zimene ziri zotsutsana ndi Mawu a Mulungu. Lero, atumiki a magulu awo amawalola anthu kuti azisewera makadi mmipingo, ambiri a iwo. Tsopano, izo zonse pamodzi si Chikatolika, pali a Chiprotestanti ambiri amene amapanga zimenezo.

⁷¹ Chimene iwo ayesera kuchita ndi chinachake chongolowa m'malo. Iwo anayesera kutenga dongosolo lina latsopano. Iwo anayesera kutenga maphunziro, kuti atenge malo a Mzimu Woyera. Inu simudzakwanitsa konse kuchita zimenezo, ziribe kanthu kuti anthu anu ndi ophunzira chotani. Ine ndikuganiza ndi chinthu chabwino kuti iye aphunzire. Koma ngati iye alibe Mzimu Woyera ndi izo, maphunziro ake samuchitira iye ubwino uliwonse. Maphunziro sadzatenga konse malo a utsogoleri wa Mzimu Woyera. Amen.

⁷² Zindikirani, iwo, mmalo mwa Ichi, iwo ayesetsa kutenga kugwirana chanza kutenga malo a chokuchitikira chachikale chimene ife tinkakhala nacho. Lero mpingo wasanduka wamakono. Iwo amayenda ndi kudzapereka dzanja lawo lamanja la chiyanjano, ndipo umo ndi mmene iwo amachitira izo. Koma izo sizidzatenga konse malo a mpando wa olira achikale pamene ochimwa ankaitanidwa ndipo ankazikonza ndi Mulungu. Uko nkulondola.

⁷³ Lero iwo akuyesera kuti atenge malo a chakhumi cha Mulungu. Iwo akuyesera kutenga chinachake. Iwo akuyesera kuti azipange izo kukhala mosiyana. Iwo amapita kumusi ndi kukakhala ndi masewero a bunco mmipingo, kumasewera njuga. Njuga siidzatenga konse malo a chakhumi cha Mulungu.

Maphwando a usiku, kugulitsa mabulangete, masanje, kuti atolere ndalama yolipirira ngongole zina, izo sizidzatenga nkomwe malo a chakhumi cha Mulungu Chamuyaya ndi chopereka. Izo sizidzachita nkomwe zimenezo. Komabe ife timayesetsa kumachita izo.

⁷⁴ Icho ndi chiyani? Ndi mizimu yodolola ikutsika pansi, ikuyesetsa ku-...kuyikapo chinachake mmalo mwa Mawu a Mulungu. Mulungu alibe mlowa mmalo wa Mawu Ake. Iwo ndi Amuyaya ndi kwanthawizonse. Mulungu alibe kalikonse kolowa mmalo mwa chikhulupiriro. Chikhulupiriro chiribe mlowa mmalo. Chiyembekezo sichidzatenga konse malo a chikhulupiriro. Chikhulupiriro ndi chapachokha. Icho chimayima pachokha. Icho sichidzatenga konse... Chiyembekezo sichidzatenga konse malo ake. Chiyembekezo ndi chikhazikitso cha zinthu zoyembekezedwa, umboni wa zinthu zosawoneka, kapena chikhulupiriro chiri, kani. Mukuona? Chiyembekezo ndi chinthu chimodzi; chikhulupiriro ndi chinanso. Chiyembekezo chimayembekezera icho; chikhulupiriro chiri ndi icho. Chimodzi ndi chikhulupiriro cha luntha; ndipo china ndi vumbulutso lachindunji la Mulungu. Icho sichidzatenga konse malo ake. Ife tikuyesetsa, koma ife tikumapanga zolowa m'malo zonsezi.

⁷⁵ Ife tikumayesetsa kumanga matchalitchi apamwamba mmalo motumiza mamishonare. Cholowa m'malo china. Yesu sanamudzodze aliyense kuti azimanga tchalitchi. Izo sizinadzozedwepo nkomwe mu Baibulo. Ife tayikapo maseminare, iwo azilola izo kuti zitenge malo a mishonare. Ife...Yesu sanatiuze ife kuti tizimanga seminare. Zonsezo ndi zabwino. Maphunziro, akuyesera kuzitengera izo kuti atenge malo. Iwo sadzachita konse zimenezo. Kutuma kwa Yesu kunali "pitani mdziko lonse ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse," pa mapeto a nthawi. Chotero zolowa m'malo zonse zimene tiri nazo sizidzatenga malo a chenichenicho.

⁷⁶ Tsiku lina ine ndinali ndi chondichitikira, cholowa m'malo. Ine ndinali ndi kupweteka kwa dzino kwanga koyamba, ndinkayenera kuchotsa dzino. Mmawa uno ine ndiri ndi dzino lonyengezera likuwonekera pamenepo. Ine ndikumayankhula movutika. Ilo silingatenge malo a lenilenilo. Ayi, bwana! Oh, mai!

⁷⁷ Inu mukhoza kumutenga munthu ndi kumumveka iye, kumupanga iye kuchokera mu thabwa, choko, chirichonse chimene inu mukuchifuna, ndipo nkumukonza iye bwino lomwe. Iye alibe zomverera, alibe chikumbumtima. Iye sangatenge konse malo a munthu weniweni. Ngakhalenso kutembenuka kwabodza kumene kumabwera ndikuti, "Ine ndajowina tchalitchi. Ine ndiyesera kuchita bwino." Izo sizidzatenga konse malo a kutembenuka kwenikweni kwachikale, kotumizidwa ndi

Mulungu, kwa Mzimu Woyera kumene kumamupanga munthu kukhala wosiyana mu mtima mwake. Izo sizingachite zimenezo, chifukwa mulibemo Moyo mwa izo. Palibepo chirichonse choti chimupatse iye Moyo.

⁷⁸ Kuno osati kale kwambiri ine ndinawona wojambula wamkulu amene anabweretsa ichi, wosema, ine ndikutanthauza, amene anapanga chithunzi ichi cha Mose. Sindingathe kutchula dzina lake tsopano. Iye ndi waluso wa Chigriki. Zinamutengera iye moyo wake. Ndipo pamene iye anachifikitsa icho pamene iye ankaganiza kuti ndi changwiro, iye anakondowezeka kwambiri powona chithunzi cha Mose, chotero iye anamenya bondo la icho, ndipo anati, “Yankhula, Mose!” Icho chinkawoneka ngati chenicheni! Icho chinakonzedwa mwangwiro mpaka icho chinkawoneka ngati Mose, mmalingaliro ake, mpaka iye anachimenya ndi hamala kuti apangitse icho kukhala ndi zomverera.

⁷⁹ Zimaikamo mmalingaliro a mpingo. Ziribe kanthu mmene inu mungalowetsepo china, mmene inu mungakhalire ndi osonkhana ochuluka, mmene inu mumayimbira bwino nyimbo zanu, mmene osonkhana anu amavalira bwino, mmene inu muliri ndi *ichi*, *icho*, kapena *china*, inu mukhoza kumenya, kumverera, chirichonse. Icho sichidzatenga konse malo a Moyo, mpaka Khristu atatsika pansu mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, kulowa mu mpingo umenewo, ndi kuwupatsa iwo chowachitikira chatsopano chokhala wobadwa mwatsopano. Izo sizidzatenga konse malo a Mawu a Mulungu. Mawu a Mulungu amaima pawokha.

⁸⁰ Mikaya anali ndi Mawu. Iye ankadziwa kuti anali ndi Mawu. Iye anali ndi Mawu atalembedwa, iye anali nawonso Iwo mwa masomphenya. Iye ankadziwa chimene Mulungu ananena mu Mawu Ake. Iye amadziwa chimene Mulungu ananena mwa masomphenya. Iwo awiri onse anabwera pamodzi. Iye ankadziwa kuti icho chinali Choonadi, chotero iye analibe mantha.

⁸¹ Koma mzimu wodolola uwu, onani chimene iwo wachita, lero. Kuti upange mamembala a mpingo ochuluka, kuti upange mamembala a mpingo abwinoko, iwo walekelera pa chiphunzitsa cha Mzimu Woyera chakale. Iwo walola amuna kumakhala ndi maphwando oledzera wina ndi mzake, kumapita kunja pansu kumene iwo akhoza kumakasewera masewera. Izo sizidzalowa mmalo mwa chipinda chapamwamba, kumene iwo ankapempherera Mzimu Woyera. Iwo unawalola azimayi kuti abwere pamodzi ndi kumanena nthabwala ndi chinthu, ndi kumakhala ndi zovunda zambiri zimene palibepo kalikonse kwa izo. Izo sizidzatenga nkomwe malo a msonkhano wa pemphero. Akazi, mmene iwo amapitira kunja ndi kuvalira lero, ndi—ndi chamanyazi.

⁸² Ine ndinamva ndemanga imene M'bale Neville anayipanga, anati, "Anthu achi Amerika osauka," anati, "iwo atumiza zovala zawo zonse kutsidya la nyanja." Uko nkulondola. Iwo akuyenda mozungulira atavala zovala zawo zamkati. Iwo... Uko nkulondola. Iwo akuyenera kuti azipereka izo kwa amishonare, chifukwa mishonare... Anthu ndi achikunja mu dziko lina amavala zimenezo. Anthu awa akuchita opanda izo, zikuwoneka ngati akuzikonda izo.

⁸³ Ine ndikukuuzani inu, pali chinachake chimene chapotozedwa, ndipo icho ndi kulalikira kwa Uthenga wa Ambuye Yesu Khristu. Ndi ziwanda zimene zimakuvulani zovala zanu. Sipanakhalepo aliyense koma munthu mmodzi mu Baibulo amene ankang'amba zovala zawo pa iwo, ameneyo anali munthu amene anali wodzadzidwa ndi ziwanda. Ndipo iye akubwera mu mawonekedwe apansipansi lero, ngati ndi wa wamba, ngati ndi wabwino, ngati zonse ziri bwino. "Iyo ndi nyengo yozizira, ndipo izo zikupangitsa iwe kumva kuzizira ngati ngati uvule zovala zako." Mwamuma akuyenda mokwera ndi motsika pa bwalo, atavala mwatheka, ndipo akazi. Bwanji, inu mwazolowera mpaka palibeponso ulemu woposa womwe unalipo wa agalu, kwa wina ndi mzake. Vuto ndi chiyani? Ine sindikuyesera kuti ndikupwetekeni inu. Ine ndikungoyesera kukuuzani inu kuti ndi kudzadzidwa ndi ziwanda, ndipo inu mukumvetsera ku mizimu yodolola imene ikukuuzani inu, "izo ziri bwino," koma limenelo ndi bodza.

⁸⁴ Mbewu ya tirigu imangotulutsa tirigu. Ngati inu muli Mkhristu, inu simungachite zimenezo. Inu simungachite zimenezo. Inu simungachite zimenezo basi. Inu muli ndi chikhulupiriro cha luntha ndikuti, "M'bale Branham, ine ndimakhulupirira Baibulo." Moyo wanu umanena kuti inu simukutero. Ameni. Mizimu yodolola ikutsutsana ndi Mawu a Mulungu.

⁸⁵ Iye ankadziwa pamene iye anayima, Mikaya anatero. Iye anali ndi Mawu a Mulungu. Iye anali munthu wosatchuka kwambiri. Palibe amene ankamukonda iye chifukwa iye ankanena Choonadi, ngakhale kuti iwo ankawakonda alaliki awa.

⁸⁶ Tsopano, chinthu china chimene chachitika. Ine ndikukhulupirira ndipo ndikuganiza kuti mwamuna aliyense amene ali ndi chomuchitikira ndi Mulungu, kapena mkazi, ndi wokakamizika kukhala ndi zomverera pang'ono. Ine ndimangokhulupirira zimenezo. Uko nkulondola. Koma inu mukudziwa chiyani? Iwo atenga zotengeka mmalo mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Iwo amangopeza phokoso lochuluka, ndipo mulibemo kalikonse mu zimenezo. Inu mukhale basi woyera monga mwaphokoso lanulo, mukatero inu muli bwino. Zotengeka ndithudi ndi zabwino; "zolimbisa thupi zimapindulitsa pang'ono." Koma mizimu yodolola yalowerera

mu gulu lachiyero la anthu, ndipo iyo yawapangitsa iwo kuti azingodalira kuti “chifukwa chakuti iwo akhoza kufuula” kapena “chifukwa chakuti iwo akhoza kuvina, chifukwa chakuti iwo akhoza kukhala ndi kutengeka.”

⁸⁷ Mwamuna wokalamba ameneyo kumusi kumeneko, mfumu ya aneneri onsewo, alaliki, iye anali wotsimikiza kuti amalondola, mwakuti iye anadzipangira yekha nyanga ndipo anavina mozungulira, ndipo anapanga chisokonezo chachikulu. Iye ankapita kukawakankha ankhondo a Asiriya kuti atuluke mdzikolo. Koma ilo linali bodza! Mawu a Mulungu anali atanena mosiyana. Amen. Mwaona, inu mukhoza kutengeka molondola, ngati inu muli ndi kutakasika koyenera kuseri kwake, mtundu wa kutengeka koyenera kukuyendetsa kumverera kwanuko.

⁸⁸ Davide anavina pamaso pa Ambuye, ndipo mkazi wake anamuseka iye. Ndipo Mulungu anayang’ana pansu kuchokera Kumwamba, anati, “Davide, iwe ndi munthu wa pamtima Panga Pomwe.” Koma zolinga zake zinali zolondola. Moyo wake unali wolondola, kuseri kwake.

⁸⁹ Chotero, basi chifukwa choti ife tikhoza kukhala otengeka, sizitanthauza kuti tapulumutsidwa. Chifukwa choti timapita ku tchalitchi, sizitanthauza kuti ife ndi opulumutsidwa. Musamakulupirire mizimu yodolola imeneyo. Mzimu wa Mulungu weniweni, Mawu a Mulungu enieni, ndi Choonadi cha Mulungu; imene ili Mbewu ya Mulungu, idzabereka Mulungu mmoyo mwanu; khalani a umulungu, oyera mtima, opatulika.

⁹⁰ Pakati pa anthu ambiri ife timapeza pamene pali zotengeka, ndi zina zotero, pamabwera kulongolola ndi miseche, ndi mitundu yonse ya zinthu zopanda umulungu. M’bale, ameneyo ndi asidi wa chiphe mu tchalitchi. Iyo ndi mphamvu ya ziwanda. Mzimu wa amuna ndi akazi umene umabwera pakati pa wina ndi mzake, ndi kuyesera kudzachotsapo, kuti, “*Ichi* sichoyenera, ndipo *ichi* sichoyenera, ndipo *icho* sichoyenera.” Ngati inu mungachilondoloze icho, ka naini mwa teni amakhala munthu yemwe yemweyo amene akuyambitsa chisokonezo, uko sikulondola. Amen. Mulungu amadana ndi chisokonezo pakati pa abale. Muzikhala aulemu, muzikhala oyera, muzimukonda Mulungu, muziyima mbali ya Iye. Ndipo bola ngati inu mukudziwa kuti moyo wanu ukugwirizana ndi Baibulo, ndi chiyero cha mtima, chiyero cha malingaliro, chikondi kwa m’bale wako, kuyesera mopambana momwe iwe ungathere kuti umangirize Ufumu wa Mulungu, ndi kumachita zinthu zimenezo, kumavala moyenera, kumakhala moyenera, kumayankhula moyenera, kumapita ku malo oyenera, ndiye inu mukhoza kukhala ndi kutengeka konse kumene inu mukukufuna, ndipo aliyense azikhulupirira izo.

⁹¹ Yesu anati, “Ndinu mchere wa dziko. Ngati mchere wataya kukoma kwake, iwo kuyambira pamenepo ulibe ubwino,

utaidwe ndipo uponededwe ndi mapazi a anthu.” Ngati inu muli mchere panokha, iwo ulibe ubwino. Koma ngati inu muli ndi chokometsa mkati mwake, inu mukhale amchere ndipo dziko lizichita ludzu. Inu mukhale amchere, iwo akhala ndi ludzu. Oh, mai!

⁹² Mizimu yodolola kumapita, ziwanda kumaziziimbaita. Onani, ife tiri mu tsiku lotsiriza. Ife tiri kumapeto a nthawi. Dziko langokonzeka kuti libwere ku mutu wake, ngati thuza penapake limene litaphulike limodzi la masiku awa ndipo chamkaticho nkutuluka kuchoka mwa ilo. Izo zasanduka zonyansa. Palibepo mankhwala amene angachiritse izo. Iwo akana a—mankhwalawo. Iwo akana mankhwala. Inu mutenge thuza likukula pamenepo, ndipo ngati inu simutenga peniselini kapena chinachake choti chichotse ilo, kapena china chakenso, ilo lizingokula mpaka ilo liphulika.

⁹³ Izo ndi zimene dziko lachita. Ilo linayamba, osati kale kwambiri, kulekelera. Iwo anachoka pa lingaliro lalikulu lopambana, mizimu yabodza inalowa ndipo inayamba kuwauza anthu *ichi*, *icho*, kapena *china*. Ife tinagawanikana mu zipembedzo naini handiredi ndi zina zosiyana, chirichonse chiri ndi ganizo losiyana. Iwo amati, “Ife timakhulupirira *ichi*, basi! Ndi zonse zimene ife timazikhulupirira.” Iwo sangalole Mzimu Woyera kuti ulowe. Iwo sangakhale ndi njira yoyenera. Mulungu ali ndi gulu la anthu amene angafuule, ndiye aliyense amayenera kufuula. Iwo ali ndi ena amene amayankhula malirime, ndiye aliyense amayenera kuyankhula malirime. Iwo ali ndi zonse monga *ichi*, mpaka *icho* chakhala (chiyani?) mtheradi chodetsedwa ndi mizimu yodolola, kuwakopa anthu kuti apange zomverera izi pamene mulibemo Mulungu mu zimenezo nkomwe. Kenako iwo amapita kunja ndi kukakhala moyo wa mtundu uliwonse umene iwo akufuna kukhala, ndipo kenako nkumadzitcha izo “Mkhristu.”

⁹⁴ Ndipo dziko limakhala ndi kumayang’ana, ndikuti, “Chabwino, tayang’anani pamenepo! Ine ndiwabwino chimodzimodzi monga momwe iwo aliri.”

⁹⁵ Monga ine ndinanenera usiku wina zokhudza nkhumba, zokhudza wochimwa. Inu simungamunene. . . Wochimwa ndi wochimwa. Musayesere kumukonza iye. Musayesere kumuuza iye *ichi*, *icho*, kapena *china*. Iye ndi wochimwa, kuyamba ndi kuyamba. Iye ndi nkhumba, kuyamba ndi kuyamba. Iye samadziwa kusiyana. Ngati iye amapita ku makanema, ndipo iye amapita Lamlungu, ndipo iye amapita ku masewera a mpira, ndipo iye amapanga zinthu zonsezi, iye ndi wochimwa, kuyamba ndi kuyamba. Chikhalidwe chake ndi changati cha nkhumba. Nkhumba yakaleyo imalowetsa mphuno yake pansu pa mulu wa manyowa ndi kudya chimanga chonse pamenepo, ndi chirichonse; chabwino, izo, iyo ndi nkhumba. Inu simungainene iyo. Iyo ndi nkhumba. Umo ndi mmene ziriri ndi ochimwa. Koma

pamene iwe upita ndi kumadzitcha wekha Mkhristu, ndi kuyika mphuno yako ndi iye, ndiye iwe siwabwino kuposa mmene iyo iliri, koma, iwe wayipa kwambiri. Tulukani pakati pa izo. Zisiyeni za mdziko zizipita. Zisiyeni zizipita. Muloleni Mulungu. Zisiyeni zizipita.

⁹⁶ Inu mumazisiya bwanji? Anthu ambiri akudabwa lero, akuti, “Chabwino, M’bale Branham, inu mumasiya chotani?” Ine ndikudziwa inu munamva za fioloje zochulukana pa izo, “zisiye.” Anthu ambiri amangotuluka thukuta, akuyesetsa kuti azisiye zizipita. Anthu ambiri amabwera ndikuti, “Ine ndimati ndikhale ndi kusala kudya kwa masiku forte kuti ndipange chinachake.” Inu simukusowa kusala kwa masiku forte. Inu mukuyenera muzisiye za mdziko ndi zinthu za mdierekezi izi, ndi kuwatengera Mawu a Mulungu mu mtima mwanu. Inu mukuyenera kuphunzitsidwa mmene mungachitire izo. Inu simuchita izo podumpha chokwera ndi chotsika, komanso simuchita izo pa kusala kudya kwa masiku forte. Inu mumachita izo ndi mtima wodzipereka kwa Mulungu Wamphamvuzonse.

⁹⁷ Monga khanda laling’ono. Ine ndinazindikira khanda langa kumbuyo uko, amayi ake akuyesera kuti amuveke jekete yake yaing’ono, mmawa uno. Iye amafuna kuti alowetse nkono wake waung’ono mu nkono wa jekete. Iye amakanika kulowetsa nkono wake mmenemo; iye samadziwa mmene angachitire. Inu mukuyenera kutsogolera nkono wake waung’ono. Iye amafuna kuti alowetse mkono wake mmenemo, koma iye amangomenya mozungulira iyo. Iye samafika nkomwe ku nkono wa jeketeyo. Iye amadziwa kuti sali mu nkono wa jeketeyo.

⁹⁸ Ndipo chimodzimidzinso inu mumadziwa kuti inu simuli oyenera ndi Mulungu, pamene inu mukupangabe mabodza, kunama, kupanga chirichonse. Inu simungakhale olondola ndi Mulungu, ine sindikusamala kuti inu muli ndi mipingo ingati, mpaka solo yanu itatembenuka. M’bale, zimenezo nzachikale, koma zidzabwata ndi kuyika supu mu solo yanu. Kulondola!

⁹⁹ Kuyesera kulowetsa nkono wake, iye akuyenera kukhala ndi winawake woti amulondolere iye, mmene iye angalowetsere nkono wake. Kenako pamene iye alowetsa mkono wake mu jekete yaing’ono, iye amadziwa kuti ali bwino.

¹⁰⁰ Umo ndi mmene izo ziriri ndi Mkhristu wobadwa mwatsopano aliyense. Pamene iye amalowa kwenikweni mwa Mulungu, iye amawona moyo wake ndi Mawu a Mulungu ndipo iye amazindikira kuti walumikizana ndi gawo lililonse la Iwo. Iye ali ndi kuleza mtima, chifundo, kudekha, chifatso, mphamvu, chikhulupiriro, chikondi, chimwenwe, mtendere. Iye samangokankhidwa ngati nyanja yovutitsidwa. Iye samadandaula za kanthu kakang’ono kalikonse. Iye samadumpha *apa* ndi *apo*, ngati chotsekera botolo pa nyanja ya mphepo. Iye ndi wokhazikika. Mtima wake ndi woyera.

Malingaliro ake ndi oyera. Zolinga zake ndi zoyera. Lingaliro lake ndi loyenera. Ndipo iye amadziwa kuti amagwirizana ndi Mawu a Mulungu. Gehena yonse singamusunthe iye. Iye walumikizidwa ndi Mawu a Mulungu. Iye ali ndi chikondi Chaumulungu, chiyero mu mtima wake, kwa mwamuna ndi mkazi aliyense. Iye ali. . . Iye amakanizidwa zinthu za mdziko, izo ndi zakufa kwa iye; iye sakuzifuna izo kenanso. Bwanji, inu simungamupange mtsikana wa Mzimu Woyera kuti avale zovala zowoneka popanda umulungu zimenezo ndi kutuluka kunjira kumeneko popanda kanthu. Ayi, bwana.

¹⁰¹ Tsopano, palibe chifukwa chopita ndi kukamuuza iye kuti akulakwitsa, chifukwa iye sakukhulupirirani inu, chifukwa izo ndi zowe zimene iye amadziwa. Chimenecho ndi chimwemwe chake. Mkazi amavala zinthu zazing'ono zimenezo; iwo amatuluka, madzulo, basi pamene amuna akupita kwawo; iwo amabwera kuti adzatchetche pabwalo, chotero monga. . . Ndipo mukundiiza ine kuti zimenezo ndi zoono? Mkazi, ine sindikutanthauza kunena kuti ndiwe—ndiwe woyipa. Ine sindikutanthauza kunena kuti ndiwe wopanda khalidwe. Koma iwe sukuzindikira, mlongo, kuti mzimu woyipa wakugwira iwe. Iwe ungachite izo chifukwa chiyani? Iwe uli ndi nzeru zokwanira kudziwa kuti izo sizozizira. Izo ndi zotentha. Pali mzimu woipa.

¹⁰² Inu mukuti, “Ine? Ine, ine ndinapita ku tchalitchi!” Nebukadinezara anali mwamuna wopambana. Koma, chifukwa iye anayamba kudzikweza, Mulungu anamupatsa iye mzimu wa ng'ombe, ndipo anamulola iye kuti azidya udzu kwa zaka seveni, ndipo zikhadabo zake zinakula ngati ena a atsikana awa mozungulira kuno. Uko nkulondola. Ndipo iye anadzazidwa ndi ziwanda.

¹⁰³ Munthuyo anadzazidwa ndi ziwanda ndipo anavula zovala zake. Iwo sakanatha kumuveka iye zovala. Kodi inu mukuwona chimene ine ndikutanthauza? Ndi mizimu yodolola.

¹⁰⁴ Mpingo wanu umagwirizana nazo izo. Mlaliki wanu amawopa kunena chirichonse, amawopa kuti inu simuziperekanso zakhumi zanu. Chifukwa chake ndi chimenecho. Vuto lake ndi limenelo. Mai, kalanga! Inu mungalalikire bwanji ku gulu la akhwangwala, pokhapokha inu mutawapangitsa iwo kuti atembuke ndi kuyanjana ndi Mulungu, kuyamba ndi kuyamba? Iwo amazika mphuno zawo mu zinthu zakufa nthawi zonse. Chimene inu mukuchisowa ndi kutaya, ndipo chipembedzo chakale chisese kuchokera ku gombe kupita ku gombe, ndi kuwapangitsa amuna ndi akazi ayanjane ndi Mulungu. Masulani, zinthu za mdziko! Masulani, kulalikira kozisisita. Ameni. Lalikirani Uthenga. Mulungu ananena chomwecho. “Ngati inu mulikonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.”

¹⁰⁵ Anthu akhoza kumadumpha chokwera ndi chotsika, ndi kumafuula usiku wonse, ndi kuyankhula mmalirimu ngati akuthira nandolo pa malo odyera ng'ombe owuma; nkuchokapo, mmawa wotsatira, ndi kupysamtima kokwanira komenyana ndi macheke, kupita kunja ndi kukanena chinachake mu tchalitchi chimene chitapangitse mpingo wonse kuphwasuka. Izo si china mu dziko koma mizimu yodolola, yaziwanda! Ndikufuna ndibwerere ku Mawu, kumene Mulungu ndi chiyero, woyera. Amen. Uko nkulondola. Ziwanda zodolola kutsutsana ndi Mawu a Mulungu!

¹⁰⁶ Apa pali munthu, osati kale kwambiri, anali ndi mkazi wachichepere... Akatolika ali nawo dazeni kumeneko. Mu nthawi yake ya kusintha thupi, izo zimatulukira mmanja mwake ndi pachipumi pake. Ngati mlaliki wabwino wa Mzimu Woyera... ine ndinaganiza. Mwamuna ameneyo anali ndi botolo la zinthu zimenezo, mmanja mwake, akuyenda kumazungulira pamenepo kumawazodza anthu ndi zimenezo. Psyii! Chifundo! Ndi wotsutsakhristu! Ine sindikusamala ngati magari akuchokera mphuno mwake kapena kuchokera mmutu mwake, kapena pati, m'bale, palibepo magari amene angatenge malo a Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. Amenewo ndi Magazi okhawa amene ine ndikudziwa chirichonse cha iwo. Iye mwina akhoza kuti anali ndi mafuta akutuluka kuchoka mdzanja limodzi, ndipo vinyo kuchokera mu lina, koma, ngati inu mungagwiritse izo mu mawonekedwe aliwonse a chipembedzo, ameneyo ndi mdierekezi. Kuwona mmene alaliki angatsatirire chinthu ngati chimenecho!

¹⁰⁷ Chimene ife tikuchisowa, kubwerera ku Bukhu la Namulondola, kubwerera ku Mawu a Mulungu! Awa ndi Mawu a Mulungu, Baibulo lodala lakale. Mukuti, "Chabwino, ine ndikuwopa kudzakhala zimenezo, M'bale Branham. Ine ndikuwopa kuti ine nditaya chimwemwe changa china." Vuto ndi chiyani? Inu simukudziwa chimene chimwemwe chiri.

¹⁰⁸ Ine ndanena kuti sindimadzudzula woledzera chifukwa chopita kunja ndi kukaledzera. Iye amakhala wolunda yense. Iye sakudziwa. Iye amadzuka, mmawa, iye amakhala waledzera, wamatsire. Amapita kunja ndi kukadzitengera mabotolo awiri kapena atatu a mowa, ndipo amatuluka ndi kukadziphezera kachaso wina, ndi mtundu wa zinthu zimenezo.

Wosuta ndudu wamng'ono amakhala pansu ndi kusuta, ndi kutulutsa kuchokera mphuno mwake ngati kuti iyeyo ndi sitima. Ndizo zonse. Ine sindikumunena iye; chimenecho ndi chimwemwe chonse chimene iye amachidziwa. Ndizo zonse zimene iye amazidziwa. Iye ndi nkhumba, mwa chikhalidwe.

¹⁰⁹ Manyazi kwa inu amene mumadzinenera kuti ndinu Mkhristu ndi kumadalira pa zinthu zoterozo ngati chimwemwe, pamene Uthenga wa Mzimu Woyera si china koma nyumba

yamphamvu imodzi ya chimwemwe. Uthenga wa Mzimu Woyera ndi mankhwala angwiro kwa munthu aliyense amene ali ndi matsire. Inu mumamwa Uthenga wa Yesu Khristu, kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera, inu mwaledzera mpaka mutachoka mu dziko ili, ameni, chimwemwe chosaneneka ndi chodzadza ndi ulemelero. Pali kukondoweza kopitirira. Iko ndi kuledzera kosalekeza, kuledzera masana ndi usiku! Ameni. Amenewo ndi Mawu a Mulungu.

¹¹⁰ Mpingo umabwera mozungulira, umatenga chinthu china. Iwo amayenera kukhala ndi phwando laling'ono kumene iwo onse amapita kunja mmbali mwa nyanja, kuti akasangalale. Phwando la makadi losonkhana pamodzi, ngati chiyanjano. Uko nkulondola. Kukhala ndi zovina, nthawizina, ku nyumba ya membala mmodzi, nthawizina mu chipinda chapansi cha tchalitchi. Zovina, kutenga, kuyesera kutenga chinachake choti chiwakhutitse. Vuto ndi chiyani? Iwo ndi gulu lalikulu la nkumba, mulimonse. Iwo ndi nkumba, kuyamba ndi kuyamba. Ngati iwo anakalumikizana ndi Khristu, iwo akanakhala ndi chimwemwe chochuluka, zinthu zimenezo zikanakhala zakufa kuposa pakati pa usiku, kwa iwo. Uthenga, kuledzera Mzimu, chimwemwe chosaneneka ndi chodzadza ndi ulemelero.

¹¹¹ Musamamutsutse wochimwa; muzimuchitira iye chifundo. Muloleni iye azipitirira ndi kumasuta paipi yake, muloleni iye azimwa mowa wake, muloleni iye azikhala ndi phwando la makadi lake. Izo ndi zomusangalatsa zake. Musamamunene iye. Akubwera kunyumba ndi chirichonse, wotopa ndi wotheratu, iye amafuna chosangalatsa china. Chinthu choti inu muchite ndi kukhala moyo wa umulungu umene inu mungatsimikizire kwa iye kuti Uthenga umagwira kuchulukitsa ka teni sauzande kuposa izo, kwa iye. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Ndipo ngati iye angafe mu chikhalidwe chimenecho, iye adzapita ku gehena, ali pa kachaso wake. Kumeneko ndi kuledzera kwa mdierekezi. Ngati iye angafe, akukoka paipi yakaleyo, Mulungu ndi woweruza wawo. Ngati iye angafe, akupita kunja kuno, akuvina, ndi kumathamanga mozungulira atavala zovala zadama, Mulungu ndi Woweruza wawo.

¹¹² Koma pali chinthu chimodzi, ngati inu mungafe pansi pa Mphamvu yodzoza ya Mzimu Woyera, monga Stefano anachitira pamene iye anayang'ana mmwamba pamaso pa Mulungu, anati, “Ine ndikuwona Kumwamba kutatseguka, ndipo Yesu wayima ku dzanja la manja,” inu mukupita Kumwamba, ngati mtemankhuni ku bokosi lake. Ameni.

¹¹³ Mizimu yodolola ikutsutsana ndi Mawu a Mulungu! Masukani, zisiyeni zipite. “Inu mumachita izo motani, M'bale Branham?” Ingozisiyani. Ndizo zonse zimene inu mukuyenera kuchita. Mutenge Mawu a Mulungu. Musamayesere kuchita kanthu. Musamayesere kukhala pansi pa guwa ndi kumenyera

izo, kukuwa, “Mulungu, ndipatseni ine Mzimu Woyera! Ambuye, ndipatseni ine Mzimu Woyera!” Iye sakubwera, inu mukumenya pa guwa limenelo. Zimenezo sizichita ubwino uliwonse. Ayi. Umo si mmene Iwo umabwerera. Izo ndi, kumutenga Iye pa Mawu Ake!

¹¹⁴ Muoneni Petro. Petro anali mmavuto, zinkawoneka ngati iye afa. Ndipo iye anawawona Ambuye akubwera, akuyenda pa madzi. Ndipo iye anati, “Ambuye, ngati ameneyo muli Inu, ndiloleni ine ndibwere.”

Ambuye anati, “Bwera.”

¹¹⁵ Tsopano Petro anati, “Tsopano dikirani miniti, Ambuye, ndiloleni ine ndipite ku kusala kudya kwa masiku forte, kuti ndiwone ngati ine ndingayende pa madzi amenewo, kapena ayi. O Ambuye, ndiloleni ine ndikhale ndi Mzimu wokwanira pa ine, kuti ine ndithe kuvina mu Mzimu ndi kuyankhula mmalirime, mu bwato ili, kenako ine ndikhoza kutuluka”? Ayi, bwana! Iye anamutenga Mulungu pa Mawu Ake, kumasuka ndi kuzisiya zizipita. Mulungu anamudutsitsa iye.

¹¹⁶ Nanga bwanji ngati Mulungu akanakumana ndi Mose, ndipo Iye anati, “Mose, pita kumusi uko ku Igupto, ndipo ukamuze Farao, ‘Alole ana anga azipita’”? Nanga bwanji ngati Mose akanati, “Ndiloleni ine ndipite pa kusala kudya kwa masiku forte, poyamba, ndipo ndiwone ngati ndiri ndi chikhulupiro chokwanira kuti ndikumvereni Inu, Mulungu. Ndipatseni ine chinachake, chinachake chimzake, Ambuye. Ndiloleni ine ndikuuzeni Inu chinachake, ndiloleni ine ndiwone ngati ine ndingalowe mu Mzimu, poyamba”? Mose sanafunse mafunso, Iye anangomutenga Mulungu pa Mawu Ake, ndipo ananyamuka. Umo ndi mmene inu mukuyenera kuchitira, kumutenga Mulungu pa Mawu Ake. Kenako inu mumadziwa kuti mukwanitsa kuchita izo. Iye sanadikirire mpaka chinachake chitachitika, iye anangopitirira ndipo anakachichita icho.

¹¹⁷ Nanga bwanji Eliya, pamene iye anabwera kuchokera ku Phiri la Karimeli, anali ali kumeneko kwa nthawi yaitali? Ndipo iye anakumana ndi mzimayi wamasiye wosauka. Iye anali. . . Iye anali mlendo, Wamitundu. Ndipo pamene iye anakumana naye kumusi kumeneko, iye anali akutola mitengo yina, kuseri. Ndipo Mulungu anamuza iye, “Pita kumusi kumeneko ku nyumba ya mkazi wamasiye ameneyo.” Ndi malo otani oti mlaliki nkupitako!

¹¹⁸ Apa iye akupita kumusi kumeneko kunyumba ya mkazi wamasiye. Ndipo pamene iye anatero, iye anali ndi nkhuhi ziwiri. Anati, “Iwe ukuchita chiyani?”

¹¹⁹ Anati, “Ndikutola nkhuhi. Ine ndiri ndi ufa wokwanira kuti ndipange zigumu zingapo. Ndizo zonse zimene ine ndatsala nazo. Padutsa zaka zitatu chikhalireni ndi mvula.” Ndipo anati,

“Ndiye ine ndipanga zigumu izi. Ndipo ine ndi mnyamata wanga tidya izo, ndi kufa.”

¹²⁰ Iye anati, “Ndipangire ine imodzi, poyamba!” Aleluya! Oh, ine ndikudziwa ine ndi wamisala pang’ono, koma ine ndiri mbali ya Ambuye, mulimonse. Anati, “Ndipangire ine imodzi, poyamba. Pakuti, PAKUTI ATERO AMBUYE.” Ndi zimenezotu.

¹²¹ Ndi chiyani chimenecho? “Yambani mwathanga Ufumu wa Mulungu, ndi chirungamo Chake.” Osati Ufumu wa Mulungu ndi “phokoso pang’ono,” osati Ufumu wa Mulungu ndi “kutengeka pang’ono,” osati Ufumu wa Mulungu ndi “chaching’ono *ichi* kapena *icho*.” Koma, “Mulungu, ndi chirungamo Chake, ndipo zinthu zina zonsezi zidzawonjezedwa kwa inu.” Muyike poyamba!

¹²² Tsopano, mkazi wamasiye ameneyo anamva zimenezo. “Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva Mawu.” Iye anati, “Amenewo ndi Mawu a Ambuye, pakuti ameneyo ndi mwamuna woyera wa Mulungu. Ameneyo ndi mneneri wa Mulungu, ndipo ine ndikudziwa icho ndi choonadi. Ndipo amenewo ndi Mawu a Mulungu.”

¹²³ Tsopano, iye sanathamange kukawafunsa oyandikana nawo mmene angachitire izo. Iye sanafune kuti apite ndi kukagawa wake. . . ndi kukawauza oyandikana nawo, ndikuti, “Tsopano, iwe ukuganiza chiyani? Mlaliki ali kunyumba kwanga, akunena izi. Susie, iwe ukuganiza chiyani za izi?”

¹²⁴ Iye analowa mkati, anakayamba kutaya. Iye anazilola zizipita. Iye anazilola zizipita zimene anali nazo, kuti apeze zochuluka. Izo ndi zimene dziko likusowa lero, kulolera kuti zizipita kwabwino kwachikale kwa zimene iwe uli nazo. Aleluya! Iye anataya, kuti iye adzadzidwe. Iye anataya mafuta onse amene anali nawo, ndi mafuta onse amene iye anali nawo ndi ufa wonse umene iye anali nawo, kwa mlalikiyo, ku Ufumu wa Mulungu. Ndipo pamene iye anataya zonse mmenemo, Mulungu anadzatsika pansu, anadzadzitsa dengo la ufa, anadzadzitsa botolo la mafuta. Iye anadzaperekanso izo kachiwiri, m’mbale ya mlalikiyo. Ndipo Iwo unabwera, unadzadzitsanso izo. Iye anaponyera mkati. Nthawi iliyonse imene iye amapereka, Iye amadzadzitsa.

¹²⁵ Ine ndinena, lero, ngati munthu angataye zamkutu zonse izi za kungotengeka, ndi kumanyengezera Chikhristu, ndi kulola Mzimu Woyera utenge malo Ake, payambika chitsitsimutso pa Eighth and Penn Street chimene chingasese dziko lonse. Siyani zamkutu. Bwererani ku Mawu a Mulungu. Tayani, kuti mudzadzidwe. Inu muzisiye zizipita, ndipo Mulungu alola zibwere. Inu mutayire kunja, Mulungu adzadzazitsamo. Zinthu zonse zopanda pake, za, “Inu mukuyenera kuchita *ichi*, ndipo mukuyenera kuchita *icho*; ndipo inu mukuyenera kuchita *ichi*

ndi kuyenera kuchita *icho*.” Muiyiwale izo! Zitayeni izo kuchoka mu solo yanu!

¹²⁶ Munene, “Mulungu, ndiloleni ine, kuyambira wamphumphu uyu. . . lero, ndikhale Wanu wamphumphu. Ambuye, ine ndikubwera ndi mtima wosweka. Ine ndikubwera ndi mzimu wosimidwa. Ine ndimakukondani Inu. Inu mukudziwa ine ndimakukondani Inu. Ndipo ine ndikufuna ndiiwale zopusa zonsezi za kusala kudya masiku forte uku ndi kuona ngati ndingabwere pafupi ndi Mulungu, ndi zonse *izi, izo, zina*, zamkutu zonsezi.”

¹²⁷ Zisiyeni izo! Palibepo chirichonse mu Mawu chimene chimakuuzani inu kuti mukhale ndi kusala kudya kwa masiku forte. Palibepo chinthu. Palibepo chirichonse mu dziko chimene chimakuuzani inu kuti musale kudya, pokhapokha Mulungu atakuuzani inu. Ngati inu mungasale kudya, inu simumva njala, ndi zinthu zonsezi. Pamene inu mukusala kudya, m’bale, iwe umakhala wachimwemwe ndi wokondwa nthawi zonse. Anati, “Musamawoneke pamaso pa anthu mmene onyenga amachitira, ndi nkhope yaitali, yokhumudwa. ‘Ine ndiri pa kusala kudya kwa masiku forte. Mbale zanga sizindikwanira ine konse. Ine ndataya mapaundi sarte, ndipo iwo anandiuzza ine kuti ndiwoneka bwino izi zikatha.’” Oh, zamkutu! Iyo ndi mizimu yodolola ya mdierekezi.

¹²⁸ Bwerani pa guwa, ndipo mudzanene “ulemelero, ulemelero, ulemelero” mpaka inu osathanso kunena china chirichonse, ndi kuti, “Inu mukuyenera kuyankhula mmalirime musanalandire Mzimu Woyera.” Zamkutu! Zitayeni zimenezo!

¹²⁹ Zichotseni zimenezo mu zochitika zanu ndipo mubwere pa Mawu a Mulungu! Iye anati, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Mulungu samasunga Mawu Ake, Iye si Mulungu. Amen. Zitayeni. Dzadzidwani. Amen. Psyii! Ine ndikuzikonda zimenezo. Amenewo ndi Mawu Ake. Mulungu anatero. Uko nkulondola. Ndipo pamene Mulungu wanena zimenezo, Mulungu asamalira zimenezo. Chabwino. Zokonzekera zonse zimene inu mumazipanga, kupita ku tchalitchi konse kumene mungapange. . .

¹³⁰ Izo ziri ngati kumusi kuno kokonza magalimoto kumene iwo amapanga mulu waukulu wa katundu, kapena, mulu waukulu wa galimoto zokwera anthu. Ine ndinkagwira ntchito kumeneko. Ndipo iwo amatenga ndi kupanga ma basi aakulu amenewo ndi chirichonse, ndi kuyika thabwa lolimba, m’bawa woyikidwa mozungulira paliponse, ndipo chirichonse chokongola kwambiri, ndi kuyika iwo pa msewu, ndipo iyo inali yakufa ngati msomali wapa chitseko. Pamenepo panali injini, yopanda nthunzi mwa iyo. Iyo inangokhala pamenepo.

¹³¹ Chomwe ikusowa lero ndi moto mobwatitsiramo. Chimene iyo ikusowa lero ndi nthunzi ina. Chimene iwo ukusowa lero, mpingo, kuti ubwate; kubwatitsa kotentha kwambiri kumene kulipo kuti kubwatitse tchimo kuchoka mmoyo mwanu, ndi chikondi. Ndipo ngati inu simungakondane wina ndi mzake, inu mungamukonde bwanji Mulungu Amene simunamuonepo? Chikondi chimabisa unyinjira wa tchimo. Lowani mu chikondi ndi Mulungu, mukatero inu mudzakondana wina ndi mzake, kenako inu mudzawukonda mpingo, mudzakonda Cholingacho, mudzakonda chirichonse chimene chiri cha umulungu, ndipo mudzatalikirana nazo zinthu za mdziko.

¹³² Mizimu yodolola ikupita mozungulira kumakawauza anthu *ichi, icho*, kapena *china*, “Iwo akuyenera kuchita *ichi*. Iwo akuyenera kuchita *icho*.” Ndi chifukwa choti zipembedzo zadzukupita, ndipo iwo ali ndi vumbulutso laling’ono limene iwo amati, “Chabwino, tsopano, ine ndikukhulupirira kuti munthu. . .Ine ndimakhulupirira mu chinthu chotero ngati kufuula mu Baibulo.” Uko nkulondola. Icho ndi choonadi. Iwo anapanga chipembedzo kuchoka mu izo, “Pamene inu mufuula, inu mwawulandira Iwo.” Koma inu simunatero.

¹³³ Wotsatira anadzuka, ndikuti, “Kuyankhula mmalirime.” Uko nkulondola. Izo ziri mu Baibulo. “Chabwino, pamene inu muyankhula mmalirime, inu muli nawo Iwo.” Koma ambiri a iwo anayankhula mmalirime ndipo analibe Iwo. Mukuona? Zimenezo si Iwo. Ayi, bwana.

Ambiri a iwo anati, “Chabwino, ife tikuyenera kunenera.”

¹³⁴ Awoneni aneneri awa apa ali ndi nyanga pa mutu wawo, akudumpha mmwamba ndi pansa ndi kumanenera. Mikaya anati, “Inu, aliyense, mukunama.” Amen. Kulondola. Mulungu samabwera moteromo. Mulungu amabwera ku mtima woona umene umabwera ndi mzimu wosimidwa, wosweka. “Iye amene apita patsogolo, akudzala mu misozi, mosakayika adzabwerera kenanso akusangalala, akubweretsa ndi iye zoweyula zofunika.” Amen. Umvetse zimenezo, mzanga.

¹³⁵ Za ziwanda zochulukira, ziwanda zikugwira ntchito mu solo ya munthu! Onani pamene izo zikubereka chipatso chake. Onani mtundu wa moyo umene munthu akuukhala. Muone mmene iwo akuchitira, onani mmene iwo akuchitira, muone chimene zolinga zawo ziri. Izo ndi zosatheka basi. . .Ndipo ngati ine ndikanakuuzani inu zimenezo, “Njira yokhayo. . . Apa pali galimoto, zonse zitaikidwa apa. Kumwamba kuli ku Charlestown. Inu simungayende. Njira yokhayo imene mungapitire, ndi galimoto. Ndipo munthu aliyense amene ataoloke mzerewo akuyenera kubweretsa zigubu faivi za mafuta.” Apa pali galimoto yake, koma ngati iye alibe mafuta iye sangayendere iyo. Chabwino, ndizo ndendende, mwangwiro mmene ziriri Kumwamba. Ngati inu mungafe opanda Mulungu,

ine sindikusamala mmene inu mwakhalira ndipo ndi galimoto zingati zimene inu mwazipanga, ngati chikondi cha Mulungu palibepo choti chikukokereni inu ku Ufumu wa Mulungu, inu mwatayika.

¹³⁶ Apo pali chotsutsa ndi chovomereza. Ziribe kanthu mmene mphanvu iyi ikuyendera apa, ngati iyo ilibe waya wapansi, iyo siiwala. Uko nkulondola. Inu mukuyenera kuzikidwa, kuikidwa pansu mu chikondi cha Mulungu. Oh, m'bale! Mukayika chotsutsacho ndi chovomereza pamodzi, inu mukhala ndi Kuwala, Kuwala kwa Uthenga kwachikale kwabwino. Kuloleni Iko kumwazikane kuchokera ku gombe kupita ku gombe. Inu simudzakhala ndi Iko popanda izo. Ziribe kanthu ndi kugwedera ndi kudumphika kotani kumene inu mungapange ndi chovomereza, inu mukuyenera kukhala ndi waya wapansi woti awalitse kuwala. Amen.

¹³⁷ Inu munayamba mwazindikira? Inu mwayika waya wapansi apa pa ichi, ndipo gawo lirilonse limapita pansu kupita ku sitieshoni, kulowa pansu mu nthaka. Ndipo nthawi iliyonse munthu akazikidwa ndi kuikidwa Mmawu a Mulungu, izo zimamuzika ndi kumuyika iye pa Kalvare, uko, kumene nangula, mtengo womangira wa Mulungu unabweretsedwa kumeneko, kuti udzawalitse Kuwala kwa Uthenga. Amen.

¹³⁸ Inu mukudziwa chimene vuto liri? Anthu kosungira mitembo kozizira kwakukulu kunjira uko, akunamizira kuti akulalikira Uthenga. Mlaliki wamng'ono anabwera kwa ine dzulo, ndi wa chimodzi cha zipembezozo zopambana zimene ziripo mu dziko lero, kunjira kwa Katolika. Iye anati, "M'bale Branham, ine ndi wodwala ndi wotopa." Anati, "Iwo atipangitsa alaliki tonse kuti tizivala mwinjiro ndi kutembenuza makolala athu, ndi—ndi kulalikira zinthu zina. Ndipo iwo azitiuza ife zoti tilalikire, pa kota iliyonse." Iye anati, "Ine sindingazipirire izo konse." Iye anati, "Ine ndipange chiyani? Kodi ine ndiyambe kulalikira Uthenga?"

¹³⁹ Ine ndinati, "M'bale, pokhapokha ngati uli ndi chipembezozo chimenecho, chilemekeze icho. Iwe uzinena chimene iwo akufuna. Koma upite kwa wamkulu kapena woyang'anira wanu, ndipo ukati, 'Bwana, ine ndabadwa mwatsopano ndi Mzimu wa Mulungu. Awa ndi Mawu a Mulungu. Ngati inu mungandilole ine kulalikira Iwo, ine ndikhala mu mpingo wanu. Ngati inu simutero, ine ndapita. Utembenukire kwa winawakenso.'" Iyo ndi njira yochitira izo. Usalubwelubwe. Musakhale wotsutsa. Tulukani ndipo munene chimene icho chiri. Kulondola.

¹⁴⁰ Iye anati, "M'bale Branham, inu mukuganiza ine ndingakhale ndi mpingo?"

¹⁴¹ Iye anati, "Kumene kuli Nyama, Mphungu zidzakasonkhanako." Uko nkulondola, izo zimatsatira.

¹⁴² Ngati munthu, kamodzi, amene ankagogomola nkhuu. Tsopano, izo si nthabwala. Ine sindikutanthauza izo ngati nthabwala. Ine ndikutanthauza izo ngati mfundo. Iye ankayika nkhuu zake, ndipo iye analibe mazira okwanira. Iye anayika dzira la bakha pansi pa imodzi. Ndipo pamene iwo anagogomola, bakha anali chinthu chooneka moseketsa chimene nkhuu zinawonapo. Chotero nkhuu inkayitana nkhuuko ndipo anapiye ankabwera, koma bakha sankadziwa chinenero chimenecho. Koma, tsiku lina, nkhuu yakaleyo inawatsogolera iwo kunja kuseri kwa nkhuu. Kunali phompho kumusi kuseri kwa nkhuu. Pamene bakha wamng'ono ameneyo ananunkhiza madzi amenewo, iye anathamangira ku madzi molimba mmene iye akanapitira. Nkhuu yaikuluyo inati, “kulu, kulu, kulu.” Ndipo bakha wamng'onoyo anati, “honki, honki, honki.” Iye anapita ku madzi. Bwanji? Iye anali bakha, mwa chikhalidwe. Pamene iye ananunkhiza madzi, m'bale, iye sakanatalikirana ndi iwo, pakuti iye anali bakha.

¹⁴³ Ndipo ine ndikunena lero, munthu aliyense amene akufuna kwenikweni kumupeza Mulungu, sangalore mpingo kuwauza zinthu zimene iwo sangazikhale, *icho* kapena *china*. Ngati inu muli ndi khalidwe la Mulungu mwa inu, inu mudzapita ku chiyero. Inu mupita ku chinthu choyenera. Inu muyimira chinthu choyenera. Inu muchita chinthu choyenera. Inu muganiza chinthu choyenera. Inu mukhala chinthu choyenera. Ngati inu muli bakha, mumakonda madzi. Ngati inu muli Mkhristu, inu mumakonda Khristu. Ngati inu muli mdierekezi, inu mumakonda zinthu za mdierekezi. Ngati inu muli khwangwala, inu mumadya zinthu zakufa. Ngati inu muli nkhuu, inu muzidya manyowa. Inu muli pati lero? Kulondola. Inu mukunena kuti muli kuno, kudya zinthu za Ambuye, kenako nkupita pansi ndi kuzikika ndi mdierekezi. Pali chinachake cholakwika ndi izo. Siyani kumvetsera mizimu imeneyo; izo ndi ziwanda. Ziribe kanthu ngati inu mukuyenera kuyima panokha. Amuna ndi akazi amene sanafike ku chirichonse, pafupifupi, akhala ali amuna ndi akazi amene anayima paokha ndi Mulungu.

¹⁴⁴ Muoneni Mikaya, mmene iye anaimira pamenepo; osati ngati thanthwe la Gibraltar, koma Thanthwe la Mibadwo. Iye anati, “Ine sindiyankhula kalikonse... Ine sindikusamala chimene seminare ikunena. Ine sindikusamala chimene mpingo wanga ukunena. Ine sindikusamala chimene mfumu ikunena. Ngati iwo angadule mutu wanga, ine ndingonena chimene Mulungu wachiika pakamwa panga kuti ndinene.” Iye ankalondola. Iye ankalondola.

¹⁴⁵ Ndipo lero, amuna ndi akazi, musamakhale ndi chidwi ndi chimene dziko liri nacho kwa inu, kachitidwe kamene ilo liri nako, ndi mtundu wanji wa katamera wa bakteria amene iwo ali naye, ndipo ndikuti, “Ngati inu mutajowine mpingowo, inu mukhala bwino.” Ameneyo ndi katamera wa

bodza. Bwanji? Inu mukadali ndi nthenda ya tchimo. Uko nkulondola. Koma ine ndikuuzani inu chinthu chimodzi, m'bale, chimene chitakutetezeni inu ku tchimo, ndicho, bwerani ku Magazi ofunika a Ambuye Yesu Khristu ndipo mudzadzidwe ndi Mzimu Woyera, ndipo icho chikutetezeni inu ku tchimo lonse, ndipo zikhumbo zanu zikhala Zakumwamba, ndipo inu simukhala ndi nthawi ya zinthu za mdziko.

Tiyeni ife tipemphere.

¹⁴⁶ Atate athu a Kumwamba, pamene ife tiona mizimu yodolola iyi pa anthu, ndi kudziwa kuti iwo akunyoza zinthu za Mulungu, ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mugwira mwamuna ndi mkazi aliyense muno lero. Lolani ili likhale tsikulo, Ambuye, kuti iwo azindikire kuti moyo wawo sukugwirizana ndi Mawu. Ndipo iwo akhala akumvetsera ku chinthu cholakwika, kuti mdierekezi wakhala akuwatontholetsa iwo ndi magazini a Nkhani Yoona, zovunda zakale za mdziko, ndi zoonera za zinthunzi zoyenda ndi televizioni yodetsedwa. O Mulungu, zinthu zosatheka zotero kwa Mkhristu kuti aziyang'ane! Mulungu, izo zimatidwalitsa ife. Inu munanena kuti izo zinakudwalitsani Inu, ngati masanzi. Inu munati, "Galu amabwerera ku masanzi ake, ndipo a—ndipo nkhumba imapita ku matope ake." Galu wakale amasanza chinachake. Kumuona wobadwa mwatheka wakale, akuyenera kukhala, munthu wachinyengo atabwera paguwa, ndipo ngati kuti ulisanza dziko; kumangopitirirabe, iwo amabwerera ndi kumadya chinthucho kenanso. O Mulungu, yeretsani Nyumba Yanu, Ambuye. Aleluya! Tumizani Mzimu Woyera ndi kukhudzidwa kwachikale kumene kutayeretse chikhumbo cha munthu ndi kuyeretisa solo yake, ndipo muyeretseni iye ndi kumupanga iye cholingedwa chopita Kumwamba. Mupatseni iye. . . Konzaninso unyamata wake ndi malumbiro ake ngati mphungu, kuti iye apite mmwamba ndi kudutsa zinthu za mdziko ili, ndi kupita Kumwamba uko kumene iye akhoza kumaona mavuto akubwera patali. Perekani izo, Ambuye.

¹⁴⁷ Inu munawafanizira aneneri Anu ndi iwo, ngati mphungu, kuti anali ndi diso ngati la mphungu, amatha kupita mmwamba kwambiri ndi kumaona zinthu patali izo zisanafike. O Mulungu, dalitsani mpingo waung'ono uwu. Dalitsani anthu awa amene abwera kuno. Dalitsani alendo mu zipata lero. Ndipo mulole iwo adziwe kuti Uthenga uwu sumaperekedwa kwa munthu payekha, koma waperekedwa makamaka, Ambuye, kwa iwo amene akusowa kwambiri; podziwa kuti tsiku lina ife tikuyenera kudzaima limodzi mu chiweruzo cha Mulungu, ndi kudziwa kuti ife tidzakhala oyankhira podziwa Choonadi ndipo osachinena Icho. Atate, ine ndikupemphera Icho chitengedwe pa mtima uliwonse. Mu Dzina la Yesu.

¹⁴⁸ Ndi mitu yathu yoweramitsa kwa mphindi chabe, ine ndikudabwa ngati pali winawake pano mmawa uno amene

angati, “M’bale Branham, ine ndi wodwala ndi wotopa ndi zinthu zazing’ono zakale izi. Ine ndiri ndi zinthu zazing’ono zimene zakakamira pa ine kwa nthawi yaitali. Ine—ine nthawizonse ndimayankhula zosiyana ndi pokhota. Ine—ine ndikupanga zinthu zimene ine sindikuyenera kupanga, ndipo ine ndikudziwa izo. Izo sizoyenera kwa Mkhristu. Ine sindikufuna kupanga izo; Mulungu akudziwa kuti ine sindikufuna. Ndipo ine sindikufuna kumvetsera ku mzimu wakalewo kenanso. Icho ndi chinthu chimene chimandiika ine pansi moyo wanga wonse, kuti ndisakhale ndi chikondi chenicheni ndi ufulu mwa Khristu. Ine ndikufuna inu mundipempherere ine, M’bale Branham, kuti icho—icho chindichokere ine lero.” Inu mungakweze dzanja lanu? Mutu uliwonse utaweramitsidwa. Mulungu akudalitseni inu. Oh, mai, manja ochuluka! Zinthu zazing’ono zakale, zinthu zazing’ono zakale zimene zimakupangitsani kuyankhula kapena kuyamba mtundu winawake wa kukangana pang’ono mu tchalitchi, zimene zimakupangitsani inu kutenga mbali ndi chinachake monga choncho. Oh, izo si umulungu. Izo ndi kusagwirizana pakati pa abale. Ndipo musamachite zimenezo. Inu simukufuna zimenezo. Inu simukufuna zimenezo ndi zinthu zazing’ono zakale, mkwiyo waung’ono wakale ndi china chirichonse, choti chikuyikeni inu pansi.

¹⁴⁹ Nenani, “Mulungu, ine sindikufuna chinthu chimenecho kenanso. Ine ndi wodwala ndi wotopa ndi izo. Ine ndakonzeka lero kuzichotsa izo. Ine ndikubwera tsopano, Ambuye, ndipo ine ndikufuna ndichoke ku kudzikonda kwanga. Ngati m’bale wanga sakundichitira ine moyenera, ine ndizimupempherera iye mulimonse. Ngati abambo anga sakundichitira ine moyenera, ine ndidziwakonda iwo mulimonse. Ngati mkazi wanga sakundichitira ine moyenera, kapena mwamuna wanga, ine ndidzipita, modzichepetsa, pamaso pa Mulungu. Ambuye, ine ndikungoyang’ana pa Ufumu Wanu. Ine ndikufuna malingaliro anga olunjika. Ine ndikufuna mtima wanga wodzadza ndi chimwemwe. Ine ndikufuna ndizipita, pamene mavuto andipanikiza ine kwenikweni mondizungulira, ine ndikufunabe ndidzikhala ndi manja anga ali mmwamba ndi mtima wanga woyera pamaso pa Inu, Ambuye, podziwa ichi, kuti tsiku lina ine ndidzakumana ndi Inu. Ine ndikufuna chondichitikira choterocho. Ambuye, ndipangeni ine icho, kuyambira lero.”

¹⁵⁰ Inu mungakweze dzanja lanu, winawake amene sanakweze dzanja lake kanthawi kapitako. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mlongo, tipatseni ife poyambira pang’ono pamene ife taweramitsa mitu yathu. Inu mumatanthauza izo mochuluka bwanji? Musasewere tsopano. Iyi si nthawi yosewera. Iyi ndi nthawi yolandira. Iyi ndi nthawi imene inu mukuyenera kulandira Iwo. Bwerani, zitayeni izo tsopano. Inu mutero? Bwerani, perekani zonse mulinazo kwa Mulungu. Munene, “Mulungu, ine ndiribe zochuluka. Ine

ndi mkazi wapanyumba wamng'ono basi. Ine sindingapange zochulukwa, Ambuye, koma ine—ine ndikhoza kuwerenga Baibulo Lanu, ine ndikhoza kumapemphera tsiku lirilonse. Ine ndikhoza kutaya nyansi zonse zimene ziri mmalingaliro mwanga. Ine ndikhoza kutaya zinthu zonsezo. Ine ndi wolakwa wa zinthu zambiri zimene mlaliki wazinena mmawa uno, chotero ine—ine ndikuzitaya izo lero. Ine sindikuzifuna izo. Mulungu, ndidzadzeni ine ndi chikondi. Ndidzadzeni ine ndi chinthu chimene chitandipange ine kumukonda ndani wowawidwa amene ine ndiri naye. Ine ndikufuna izo kwenikweni, Ambuye.”

¹⁵¹ Pamene iye akuyimba apa, kodi inu simungabwere tspano ndi kuyima pa guwa mphindi chabe, pamene ife tikusonkhana ndi mawu a pemphero. Ngati inu mukutanthauza izo tspano, ngati inu mwakonzeka kusiya izo, simuchoka paguwa ili lero ndi izo mu mtima mwanu, ngati inu mungabwere moonamtima. Ndipo munene, “Ine ndikubwera pano kuti ndiyime, miniti yokha, M'bale Branham, eya, pamene inu mukupemphera ndi ine, pandekha.” Ine—ine ndikufuna inu mubwere, mupemphere. Inu mungabwere tspano? Ndi mitu yanu yoweramitsa, ndi ndani atadzuke ndi kubwera paguwa, kuyima mozungulira guwa?

Musandipitirire, O Mpulumutsi wofatsa,
Imvani kulira kwanga;
Pamene Inu mukuitana ena,
Oh, musandipitirire ine.

Mpulumutsi, Mpulumutsi,
Imvani kulira kwanga;
Pamene Inu mukuitana ena,
Oh, musandipitirire ine.

¹⁵² Ziribe kanthu mmene mwakhalira muli Mkhristu, ndipo inu mudakali ndi mizimu yakaleyo imene imayankhula ndi inu, imakulolani inu kumasuka, imakupangani inu kuyankhula za winawake. Pamene winawake abwera ndi kuyamba kuyankhula za winawake, inu mumalumikizana ndi iwo ndipo, oh, mumangowapondaponda iwo. Izo ndi zolakwika, m'bale. Musamachite zimenezo. Zimenezo zikutulutsani inu mu Dziko lolonjeredwa. Ngati inu muli ndi zinthu zazing'ono zakale zimene inu simukuyenera kukhala nazo, ngati chikondi cha Mulungu mulibe kwenikweni mu mtima mwanu, kodi inu simukhala dona ndi mwamuna, yendani ndipo munene, “Mulungu, pomwe apa ine ndizitaya izo, mmawa uno, pomwe pano. Ine ndikuchoka paguwa ili ndiri munthu wosiyana.” Kodi inu mungabwere?

¹⁵³ Kodi pali wochimwa amene sanamulandire Yesu, ndipo inu mukudziwa kuti ndinu wochimwa, inu simukumudziwa Iye ngati Mpulumutsi wanu? Inu mukuti, “M'bale Branham, inde, ine ndimaganza ndinali ndi zosangalatsa zochulukwa.

Ine ndimapita ku madansi ndi maphwando ndi zinthu zonsezo. Ine ndimawonera kanema wolakwika. Ndipo ine—ine ndimawerenga zolemba zolakwika. Ine ndimawerenga mabukhu akale amene ali ndi nkhani zonyansa. Ine ndimawoneka ngati ndimasangalala kuwerenga iwo.” M’bale, pali chinachake cholakwika ndi inu. Icho ndi chokhumba chanu; mwaona, inu mundilole ine ndione chimene munthu amawerenga, ndiloleni ine ndione chimene iye amaonera, ndimvere nyimbo zimene iye amamvera.

¹⁵⁴ Tsiku lina, ndikubwera mu galimoto, munthu winawake anandifikira ndipo anayatsa wayilesi yanga, mtundu winawake wa nyimbo zonyansa. Ine ndinati, “Thimitsa chinthu chimenecho. Ine sindikufuna kumva zimenezo.” Gwedemula winawake wakale.

Anati, “Bwanji, ine ndimakonda kumvera izo.”

Ine ndinati, “Chikhalidwe chako ndi cholakwika. Ndiwe wolakwitsa.”

¹⁵⁵ Pamene ine ndinali kunja uko, masiku angapo zitatha zimenezo, kumtunda mmbali ya phiri kapena mbali ya phiri laling’ono, ndikuwedza, ndi munthuyo. Mbalame zazing’ono zinali zikuyimba. Abakha ankakuwa. Martingale wakaleyo ankauluka mlengalenga, kapena nightingale, akuyimba matamando. Ine ndinamukuwira mnyamata ameneyo, ine ndinati, “Taona, mnyamata, izo ndi nyimbo zanga. Zisiye izo ziri zoyatsa. Imeneyo ndi wayilesi yanga. Mulungu amazitumiza izo pansu kuti zizindiimbira ine pamene ine ndiri kuno. Izo zimatontholetsa zolo yanga.”

¹⁵⁶ Zabwinoko kusiyana ndi zinthu zakale zosalongosoka, zoyimbira zakale izi zikubangula, kumapitirira, pamene inu simungadye ndi komwe pa malo a gulu. Icho ndi chakudya cha mdierekezi. Iyo ndi nyumba ya mdierekezi, zonse zasokonezedwa ndi tchimo. Kodi inu ndi omangiririka kunja kumeneko ndipo mumasangalala ndi zimenezo? Pamene iwo anayika ndalama zimenezo mu mabokosi aang’ono akale, ndipo zinthu zonse zakalezo zinabwera, inu mumasangalala ndi izo? Manyazi pa inu. Inu ndi wobwerera mmbuyo. Inu muli kutali ndi Mulungu. Inu simukumudziwa Mulungu. Ngati inu mukanamudziwa Mulungu, mu chikhululukiro cha machimo, inu simukanamvetsera ku zamkutu zoterozo. Izo zikanakhala zakufa kwa inu. Inu—inu mukanasanza izo. Inu simukuzifuna izo. Chakudya chanu ndi chabwino. Inu mumamukonda Mulungu. Kodi inu simubwera mmawa uno, kudzagwada pansu apa ndi ovomereza awa mmawa uno?

¹⁵⁷ Apa pali amuna ndi akazi atagwada apa, amene akhala ali Akhristu kwa zaka. Ine sindikuwachotsa chikhristu iwo. Koma chimene ine ndikuyesera kuchita ndi kuwauza iwo kuti mdierekezi, amene akuwalonda iwo, akuwasunga iwo

kunja kwa Chimwemwe chathunthu. Mzimu Woyera ndi Chimwemwe. M'bale, ine ndimadzuka woledzera, ndimapita kogona woledzera, ine ndimakhala woledzera tsiku lonse, woledzera usiku wonse. Oh, ine basi—ine ndimangokonda ku. . . ine ndimapita kokawedza, ine basi ndi, “Msandipitirire, O Mpulumutsi wofatsa. Imvani kulira kwanga kodzichepetsa.” Ine ndimapita kokasaka, ndi kuyimba matamando a Mulungu. Ine ndikulalikira, ine. . . kulikonse kumene ndingapite. Kodi inu simukufuna kukhala moteromo? Wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera, Iwo umakukondowezani inu. Oh, mai! Mukawamva iwo akuyimba nyimbo zakale zodetsedwazo, inu mukhoza kumayimba iyi:

Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa,
Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa;
O ndani atabwere ndi kupita nane?
Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa.

Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa,
Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa;
O ndani atabwere ndi kupita nane?
Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa.

Ndidzafika ku mpumulo wodalawo liti,
Kukadalitsika kwa nthawizonse!
Nkhope ya Atate anga ndidzaiwona liti,
Ndi kudzapuma m'chifuwa Chake?

Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa,
Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa;
O ndani atabwere ndi kupita nane?
Ndikupita ku Dziko lolonjezedwa.

¹⁵⁸ Kodi inu simubwera, mupite nawo? Ine ndikukumbukira pamene pafupifupi faifi handirede a ife titayima uko pamene ine ndinkabatiza handirede ndi twente, pafupifupi nthawi ino ya chaka, kumusi kuno pa malire a mtsinje, pamene Nyenyezi ya Mmawa yayikuluyo inabwera ikuwalira pansi pa mtsinje. Aleluya! Liwu likuyankhula kuchokera mu Iyo, linati, “Tsiku lina iwe udzafalitsa Uthenga kuzungulira dziko lapansi.” Mnyamata wosauka, wamng'ono, mbuli ya kumunda ingapange bwanji zimenezo? Chisomo cha Mulungu! Amen.

¹⁵⁹ Oh, ndani atabwere ndi kupita? Chotsani, siyani pambali, cholemetza chirichonse tsopano. Musamamvere mizimu yodolorayo. Bwerani, mumvere Mawu a Mulungu, PAKUTI ATERO AMBUYE! “Odala ndi iwo amene achita njala ndi ludzu la chirungamo, pakuti iwo adzadzazidwa.”

¹⁶⁰ Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano pamene ife tikupemphera ndi awa ali paguwa.

Ana okonedwa, ine ndikufuna inu mukumbukire, mmawa uno, inu muli pamenepo kuti musiye pambali cholemetza chirichonse. Inu muli pamenepo kuti musiye pambali cholemetza

chirichonse ndi tchimo limene limakulepheretsani mophweka. Paulo anati, mu Ahebri, mutu wa 12.

...poona kuti ife...tazunguliridwa ndi mtambo waukulu chotero wa mboni, tiyeni tisiye pambali cholemetsa chirichonse, ndi tchimo...limene silimachedwa kutifooketsa ife,...

Ndipo ine ndinganene chiyani chowonjezera? pakuti...nthawi sidza...kunena za Gidioni,... za Balac, Baraki,...za Samisoni,...za Yefita; za Davide...za Samuele, ndi za aneneri:

Amene mwa chikhulupiro anagonjetsa maufumu, anapanga chiyero, anapeza lonjezo, anayimitsa kamwa la mkango,

Anazimitsa mkwiyo wa moto, anathawa kuthwa kwa lupanga, kuchoka ku kufooka anapangidwa kukhala wamphamvu, ndipo anakuza...kulimbamtima... mdani kuthawa...

Ndipo akazi analandira akufa awo ataukitsidwa ku moyo...

Ndipo ena analandira chitonzo, nkhanza ndi matembelero,...pomweponso, zochuluka kuposa izi, ndi zomangira ndi ndende:

Ndipo—ndipo ena amene anali ndi zoyesa... kunyoza...kutembelera...

...iwo onse anapeza chonena chabwino kudzera mu chikhulupiro,...

Ndipo zonsezi, popeza chonena chabwino kudzera mu chikhulupiro, sanalandire lonjezo:

Mulungu popereka chinthu chabwino kwa ife, kuti popanda ife iwo sangapangidwe kukhala angwiro.

Chomwechonso powona ife...tazunguliridwa ndi mtambo wotere waukulu wa mboni, tiyeni tisiye pambali cholemetsa chirichonse, ndi tchimo... limatizinga ife mophweka kuti ife tithamange ndi chipiro mpikisano umene uli patsogolo pathu,

Kuyang'ana kwa Yesu woyamba ndi wotsiriza wa chikhulupiro chathu; amene ku chimwemwe chimene chinayikidwa patsogolo pake anapirira mtanda, ananyoza manyazi, ndipo... anakhala pansu pa dzanga la manja la mpando wachifumu wa Mulungu.

¹⁶¹ Yesu, mu pemphero Lake, anati, "Atate, ine ndikudziyeretsa Ndekha." Yesu anakhala woyeretsedwa, ku Mpingo. Iye akanakwatira, koma Iye sanachite izo. Iye anayeretsedwa. Iye anati, "Ayeretseni iwo, Atate, kudzera mu Choonadi. Mawu Anu ndiwo Choonadi."

¹⁶² Tsopano tiyeni tiike pambali cholemetsa chirichonse. Inu muli ndi mkwiyo? Inu muli ndi chinachake chokhudza inu, chimakupangitsani inu kuyankhula pamene simukuyenera kuyankhula? O Mulungu! Chisiyeni icho pamenepo tsopano. Chisiyeni icho pamenepo, uwoneni Moto wa paguwa ukutsika ndi kudzawutenga iwo. Onani chikondi cha Mulungu chikunyambita izo. Onani kudzikonda kwakaleko, mmene inu mumayankhulira kwa akazi anu, mmene inu mumayankhulira kwa oyandikana nawo, mmene inu mwayankhulira za anthu mu mpingo, zisiyeni izo paguwa mmawa uno, ndipo Moto wa Mulungu utsika ndi kuchotsa izo, ndipo chikondi Chaumulungu chitentha m'malo ake.

¹⁶³ Inu muli ndi matenda? Asiyeni iwo paguwa, munene, “Ambuye, ndi awa apa. Langani mwa ine mzimu woyera. Langani mwa ine mphamvu yochiritsa.” Muone chimene Mulungu atachite. Mulungu achita izo mmawa uno.

¹⁶⁴ Atate athu Akumwamba, ife tawerama mu Kupezeka Kwanu, mmalo mwa iwo amene ali paguwa. Mulole chisomo Chanu chikhale pa aliyense wa iwo, Atate. Tsopano pamene iwo. . . Ambuye, ine sindingawachitire iwo izo. Iwo akuyenera kuchita izo okha. Palibe munthu amene angawachitire iwo. Iwo akuyenera kuchita izo okha. Lolani solo yawo tsopano inene mwaokha, “O Mulungu, mkwiyo uwu, ine ndawuyika pansi apa, Ambuye. Ine sindidzawutenganso. Ziribe kanthu chimene chingabwere kapena kupita, ine ndichilora icho chipite, kuyambira lero. Lirime langa ili limene lakhala lophweka kutenga mbali ndi gulu la miseche, Ambuye, ine ndikuyiika ilo pansi apa. Ine sindidzalitenganso ilo. Yeretsani lilime langa, Ambuye. Ndiloleni ine ndimverere Angelo akubwera, monga Yesaya anachitira pamene iye anati, ‘Ine ndi wa milomo yodetsedwa. Tsoka kwa ine!’” Ndipo Mngelo anabwera, anatenga zonyamulira, ndipo anapita paguwa ndipo anatenga makala a Moto, ndipo anawayika iwo pa milomo yake ndi kumuyeretsa iye. Mulungu, yeretsani woyankhula aliyense, mmawa uno, amene amayankhula zolakwika ndi kufesa kusagwirizana. Perekani izi, Ambuye.

¹⁶⁵ Matenda onse amene awerama apa mu nyumba iyi, anthu odwala, podziwa kuti iwo ndi adierekezi, nawonso. Mulungu, ngati wantchito Wanu, ine ndikuwadzudzula iwo, mu Dzina la Yesu. Lolani iwo atuluke mwa munthu wodwala aliyense. Ndipo mulole munthu wodetsedwa aliyense, amene ali ndi malingaliro odetsedwa, oyipa, osirira, amuna ndi akazi, chimodzimodzi, Mulungu, zitulutseni izo mwa iwo. Onsewa apa akuyesera kusiya ndudu, ndi zakumwa zoledzeretsa, maphwando aang’ono, ndi zinthu zodzikonda; Mulungu, kondowezani mtima wawo ndi Mzimu Woyera mwa njira yoti zinthu zimenezo sizikhalanso ndi

chikhumbo. Izo sizikhala ndi malo; inu ndi wodzadza ndi Mzimu Woyera, kuyambira pemenepo nkumapitirira.

¹⁶⁶ Mulungu, pangani mpingo uwu ukhale tchire loyaka. Upangeni iwo malo a Mzimu Woyera, upangeni iwo Moto woyaka, kuti dziko litembenuke ndi kuona ulemelero wa Mulungu. Mulungu, muyambe ndi anthu ochepa awa, handirede angapo apa mmawa uno. Perekani izo, Ambuye.

¹⁶⁷ Yeretsani mtima uliwonse, wa Methodist aliynse, wa Baptist aliynse, wa Katolika aliynse, wa Presibateria aliynse, wa Pentekoste aliynse. Ambuye, chotsani izo mu mtima mwawo, ndipo mulole iwo abwere kwa Inu lero. Perekani izi, Atate. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, ndi kuwapereka iwo Kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu, ku kuyeretsa kwa solo yawo ndi kuchiritsa kwa thupi lawo. Amen.

¹⁶⁸ Ine ndikudabwa, paguwa, kodi inu mwasiya nkhwawa zanu? Inu mukumva ngati izo ziri pamenepo? Ngati inu mukumva kuti ziri pamenepo, inu mukhale oweruza. Inu ndi amene mukupemphera. Ine ndalalikira. Inu mupemphere. Kodi nkhwawa yanu yatsala pamenepo, m'bale, mlongo? Inu mungayisiye iyo kwenikweni pamenepo? Ngati mungatero, kwezani dzanja lanu, munene, "Inde, Mulungu, tsopano ine ndikuyisiya iyo pano. Kusiyana kwanga, ine ndikukusiya iko pano paguwa." Nanga bwanji izo, pansu kumapeto kwa guwa pano, kumanja kwanga, dona? Kodi iwe ungasiye izo pamenepo? Kodi ungasiye cholemetsa chakalecho pamenepo? Unene, "Inde, chikhulupiriro changa chikuyang'ana kwa Inu, Inu Mwanawankhosa wa Kalvare." Pamene ife tikuyimba iyo pamodzi tsopano.

Chikhulupiriro changa chikuyang'ana kwa
Inu,
Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi Waumulungu;
Tsopano ndimveni pamene ndikupemphera,
Ndichotsereni ine kulakwa kwanga konse,
Oh ndiloreni kuyambira lero
Ndikhale Wanu kwamphumphu!

¹⁶⁹ Tiyeni tiime pamapazi athu, mwaulemu kwenikweni, aliynse. Tsopano mveterani mwacheru, aliynse tsopano. Aliynse asachoke. Basi... Msonkhano sunathe. Ine ndikufuna ndipeze kuyera kwakung'ono uku, kuonamtima kwakung'ono.

Pamene njira ya moyo ya mdima ndiyenda,
Ndipo chisoni chandizungulira ine,
Inu mukhale Namulondola wanga;
Ingitsani mdima ukhale usana,
Pukutani chisoni mantha achoke,
Ndipo ndiloleni kuyambira lero
Ndikhale Wanu kwamphumphu!

Musayimbe iyo kwa oyandikana naye tsopano. Tsekani maso anu, ndipo tiyeni tiimbe iyo pang'onopang'ono, pamene ife tikukweza manja athu kwa Mulungu.

Pamene njira ya moyo ya mdima ndiyenda,
Ndipo chisoni chindizungulira ine,
Inu mukhale Namulondola wanga;
Thamangitsani mdima ukhale usana,
Pukutani chisoni mantha achoke,
Musalole ndisochere
Kuchokera ku mbali Yanu.

Ine ndiri ndi Atate uko,
Ine ndiri ndi Atate uko,
Ine ndiri ndi Atate uko,
Pa gombe linalo.

Oh, tsiku lina lowala ndidzapita ndi kumuona
Iye,
Tsiku lina lowala ndidzapita ndi kumuona Iye,
Tsiku lina lowala ndidzapita ndi kumuona Iye,
Pa gombe linalo.

Oh, tsiku lowalalo lingakhale mawa,
Tsiku lowalalo lingakhale mawa,
Tsiku lowalalo lingakhale mawa,
Pa gombe linalo.

¹⁷⁰ Ine ndikudabwa tsopano, ndi angati amene ali ndi abambo mu Dziko linalo? Tiyeni tione dzanja lanu. Ndi angati amene ali ndi amayi mu Dziko linalo? Tiyeni tione dzanja lanu. Ndi angati ali ndi Mpulumutsi mu Dziko linalo? Tiyeni tione dzanja lanu.

Uwo sudzakhala msonkhano wosangalala!
Uwo sudzakhala msonkhano wosangalala!
Uwo sudzakhala msonkhano wosangalala!
Pa lina . . .

¹⁷¹ Ine ndikufuna inu muchite chinachake. Tsopano pamene ife tikuyimba iyo kenanso, ine ndikufuna mugwirane chanza ndi winawake wayima pafupi ndi inu, ndikuti, “M'bale, mlongo, ndipemphereni ine, kuti ndidzakumane nawe mu Dziko linalo.” Musachite izo pokhapokha mukutanthauza izo. Ndi angati akufuna kudzakumana wina ndi mzake? Ndi angati akufuna kudzakumana ndi aliyense pano, Kumeneko? Ife, ndithudi tikutero. Tsopano tiyeni tigwirane chanza wina ndi mzake, ndikuti, “Ine ndikufuna ndidzakumane nawe, m'bale. Ine ndikufuna ndidzakumane nawe mbali yinayo.” Tsopano pamene ife tikuyimba iyi, “Ine ndiri ndi Mpulumutsi uko.” Chabwino.

Ine ndiri ndi Mpulumutsi uko,
Ine ndiri ndi Mpulumutsi uko,
Ine ndiri ndi Mpulumutsi uko,
Pa gombe linalo.

Oh, tsiku lina lowala ndidzapita ndi kumuona
 Iye,
 Tsiku lina lowala ndidzapita ndi kumuona Iye,
 Tsiku lina lowala ndidzapita ndi kumuona Iye,
 Pa gombe linalo.

¹⁷² Kodi izo sizikukupangani kumva bwino ndi mwabwino?
 “Yesu, ndisungeni ine pafupi ndi mtanda.”

Yesu, mundisunge pafupi . . .
 Pali kasupe wofunika,
 Waulele kwa onse, mtsinje wochiza,
 Wochokera ku Kalvare- . . .

Aliyense kwezani dzanja lanu tsopano.

Mu mtanda, mu mtanda,
 Mukhale ulemelero wanga nthawizonse;
 Mpaka moyo wanga wokwatulidwa upeze
 Mpumulo kutsidya la mtsinje.

Mu mtanda, mu mtanda,
 Mukhale ulemelero wanga nthawizonse;
 Moyo wanga ukwatulidwire
 Mpumulo kutsidya la mtsinje.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
 Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
 Nandigulira chipulumutso changa
 Pa Kalvare.

Mulungu alemekezeke!

¹⁷³ Tiyeni mwakachetechete tsopano tiweramitse mitu yathu. Ndipo mu njira yathu yokonedwa, tiyeni tingomutamanda Iye manja athu ali mmwamba, tikuti, “Zikomo Inu, Ambuye, populumutsa solo yanga. Zikomo Inu, Ambuye, pondipanga ine wamphumphu. Zikomo Inu, Ambuye, pa zonse zimene Inu mwachita, kubweretsa chiombolo chokoma, kubweretsa chipulumutso chaulele. Zikomo inu, Ambuye.” Ife tikukupatsani Inu chopereka cha mathokozo. Ife tikukutamandani Inu chifukwa Inu ndi wokonedwa kwambiri. Inu ndi Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa, Duwa la Sharon, Zonse mu Zonse. Inu ndi Atate, Mwana, Mzimu Woyera; Iye amene Anali, Amene Ali, ndipo Adzabweranso; Alfa wamkulu, Omega. Inu ndi Mmodzi Wodabwitsayo, Kalonga wa Mtendere, Muzu ndi Mwana wa Davide. Inu ndi Zonse! Ndipo ife tikukuthokozani Inu, Ambuye, pa zonse zimene Inu mwazichita. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Mawu Anu, pakuti Iwo ndi Kuwala pa njira yathu. Oh, ife tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mutilola ife tiyende mu Kuwala. Perekani izo, Atate. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Chabwino. Pamene ife tikukhala kwa miniti. “Ife tiyenda mu Kuwala.”

Tiyenda mu Kuwala, Kuwala kokongola,
 Bwerani kumene madontho a chifundo
 akuwala;
 Kuwalitse paliponse, usana ndi usiku,
 Yesu, Kuwala kwa . . .

174 Bwerani, oyeramtima, tiyeni tiimbe iyo tsopano!

Tiyenda mu Kuwala (kuyera, chiyero), Kuwala
 kokongola,
 Kumabwera kumene madontho a chifundo
 akuwala;
 Kuwalitse paliponse, usana ndi usiku,
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

Bwerani, muvomerezeni Iye ngati Mfumu
 yanu,
 Yesu, kuwala kwa dziko;
 Kenako mabelu Akumwamba adzalira,
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

Aliyense!

Tiyenda mu Kuwala (Kuwala ku njira yanga),
 Kuwala kokongola,
 Kumabwera kumene madontho a chifundo
 akuwala;
 Kuwalitse paliponse, usana ndi usiku,
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

175 Kodi izo sizikukupangani inu kumverera bwino? Ndi
 angati akumverera bwino? Ingokwezani mmwamba dzanja
 lanu tsopano, munene, “Ine ndikumverera bwino kwenikweni.”
 Mzimu Woyera wakuyeretsani inu. Kenako ife (chiyani?)
 tiyenda mu Kuwala. Musamamvetsere chirichonse. . . Kuwala
 ndi chiyani? “Mawu Anu ndi Nyali.” Chotero ndiye:

Tiyende mu Kuwala uku, ndi Kuwala
 kokongola,
 Kumabwera kumene madontho a chifundo
 akuwala;
 Kuwalitse paliponse, usana ndi usiku,
 Yesu, Kuwala kwa . . .

176 Tsopano, kodi izo sizopambana? Zikuoneka ngati
 sitingatseke. Mzimu Woyera wangotigwira ife! Inu
 simukumverera motero? Zimangomveka ngati. . .? . . .
 Zimangooneka ngati zikutuluka kunjja.

Uthenga ukuwukha magazi,
 Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi.

Woyamba kufera dongosolo la Mzimu Woyera
uwu,
Anali Yohane Mbatizi, koma anafa ngati
munthu;
Kenako kunabwera Ambuye Yesu, iwo
anamupachika Iye,
Iye analalikirira kuti Mzimu udzapulumutsa
anthu ku tchimo.

Pali Petro ndi Paulo, ndi Yohane waumulungu,
Iwo anapereka miyoyo yawo kuti Uthenga uwu
uwale;
Anasakaniza magari awo, monga aneneri
akale,
Kuti Mawu a Mulungu awuzidwe moona.

Kenako anamugenda Stefano, iye analalikirira
motsutsa tchimo,
Iye anawakwiwitsa iwo, iwo anaphwanyira
mutu wake mkati;
Koma iye anafa mu Mzimu, anapereka mzimu,
Ndipo anapita kukalumikizana ndi ena,
khamu lopereka moyo.

Iwo ukuwukhabe magari, inde, Iwo ukuwukha
magazi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magazi,
Magazi a ophunzira anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magazi.

Mvetserani!

Pali miyoyo pansu paguwa, ikulira, “Mpaka
liti?”
Kuti Ambuye alange iwo amene anachita
cholakwa;
Koma pakhala ochuluka amene ati apereke
magazi a moyo wawo
Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu
ndi kusefukira Kwake kofiira.

Ukungopitirira kuwukha magari, aleluya, Iwo
ukuwukha magari,

Ine ndikufuna ndikhale mmodzi wa iwo.

Uthenga wa Mzimu Woyera, Iwo ukuwukha
magazi,
Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magazi.

¹⁷⁷ Ine ndikufuna ndipite molunjika kuchoka paguwa. Ameni. Oh, ndi zopambana bwanji! Abale anga anapereka magari a moyo wawo. Pakhala ochuluka atachite chomwecho. Musadandaule. Izo zikubwera pa chiwonetsero pompano. Inu mwina mulowa kapena mutuluka. Iwo onse akugwirizana tsopano mu Mgwirizano wa Mipingo, ndipo onse akulowa. Iwo akugwirizana pamodzi.

Ndipo pakhala ochuluka amene atapereke magari a moyo wawo,
Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu
ndi kusefukira Kwake koyeretsa.

Ukuwukha magari, inde, Ukuwukha magari,
(Oh, aleluya!)
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magari,
Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
magazi.

¹⁷⁸ Mai! Ine ndikumverera ngati Mkwatulo basi uli pamwamba pa tchalitchi. Oh, basi zikundipangitsa ine kumva bwino kwambiri! Machimo onse ali pansu pa Magazi. Mwaona, Mzimu Woyera umakonda Mawu. Mawu ndi chimene Mzimu Woyera umadya, inu mwaona. Oh, mai! Iwo umatsika ndi kukhala pakati pa anthu, umayeretsa machimo awo, umachotsapo matenda awo, umachotsa matsire awo. Tsopano ine ndaledzera, basi kuledzera mmene ine ndingakhalire, kuledzera ndi Mzimu, chikondi chikuchoka mu mtima mwanga. Ziribe kanthu chimene aliyense anachita, icho chakhululukidwa. Mdani wanu weniweni, izo zatha. Aliyense amene anayankhulapo kapena kunena chirichonse, ngati ine. . . chabwino, ine. . . zimene zonse zapita, zonse zayeretsedwa tsopano.

Ndipo Iwo ukuwukha magari, inde, Iwo
ukuwukha magari,
Uthenga wa Mzimu Woyera ukuwukha magari,
Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
Uthenga wa Mzimu Woyera uwu. . .

Oh, mai! Ndi zopambana bwanji!

Ndi nthawi yopambana bwanji kwa inu,
Ndi nthawi yopambana bwanji kwa ine;
Ngati ife tingakonzekere kudzakumana ndi
Yesu Mfumu yathu,
Iyo idzakhala nthawi yopambana bwanji.
Nthawi yopambana kwa inu,
Nthawi yopambana kwa ine;
Ngati ife tingakonzekere kudzakumana ndi
Yesu Mfumu yathu,
Iyo idzakhala nthawi yopambana bwanji.

Inu mukuzikonda izo? Aliyense, bwerani!

Oh, nthawi yopambana kwa inu,
 Nthawi yopambana kwa ine;
 Ngati ife tingakonzekere kudzakumana ndi
 Yesu Mfumu,
 Iyo idzakhala nthawi yopambana bwanji.

¹⁷⁹ Ine ndikungomverera ngati chitsitsimutso chachikale chiri mu tchalitchi. Inu simukutero? Basi kuyeretsa kwachikale, kuyeretsa; nthawi yopambana yabwino, yakale. Kodi inu simukumva bwino? Oh!

Ndimtamanda Iye, ndimtamanda Iye,
 Tamandani Mwanawankhosa wofera
 ochimwa.

Tiyeni tiyimbe iyo tsopano, aliyense. Inu mukuyidziwa iyo? Ine ndikuyidziwa iyo. Bwerani apa; inu mundithandize ine kuyitsogolera iyo, M'bale Neville. Ndipo nonse a inu, pamodzi tsopano, mungokweza manja athu, imbani iyo, tsopano, tsopano, ngati mungathe.

Tamandani Mwanawankhosa wofera
 ochimwa;
 Mpatсени Iye ulemelero, anthu nonse inu,
 Pakuti Magazi Ake atsuka banga lililonse.

¹⁸⁰ Tsopano, aliyense, tiyeni!

Ndimtamanda Iye, ndimtamanda Iye,
 Tamandani Mwanawankhosa wofera
 ochimwa;
 Mpatсени Iye ulemelero anthu inu nonse,
 Pakuti magazi Ake atsuka banga lililonse.

Ameni. Izo ndi zopambana?

Mzinda woyera wangale,
 Ndiri ndi nyumba, zeze, ndi korona;
 Tsopano ndikudikira, kuyang'anira ndi
 kupemphera,
 Mzinda woyera umene Yohane anawuona
 ukutsika.


¹⁸¹ Amenі. Zopambana! Oh! Tsopano tiyeni tiime pa mapazi athu, aliyense. Ine ndikuyembekeza kuti mukumva bwino. Kumbukirani misonkhano usikuuno. Tsopano ife tikufuna tiimbe nyimbo yathu yabwino, yakale yobalalitsira.

Pa dzina la Yesu kugwada,
 Kudzilambatitsa pa mapazi Ake,
 Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka
 Iye korona,
 Pamene ulendo wathu watha.

Chabwino. Aliyense tsopano, pamodzi. Chabwino.

Pa Dzina la Yesu kugwada,
 Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
 Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka
 Iye korona,
 Pamene ulendo wathu udzatha.
 Dzina lofunika (Dzina lofunika), Oh kukoma
 kwake! (Oh kukoma kwake!)
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba;
 Dzina lofunika (Dzina lofunika), Oh kukoma
 kwake! (Oh kukoma kwake!)
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba.

¹⁸² Ndi mmawa wopambana bwanji! Ndi nthawi yopambana bwanji! Tiyeni tiweramitse mitu tsopano kwa mphindi. Aliyense muyang'ane molunjika kwa Khristu tsopano, Mpulumutsi wanu. Mu njira ya kachetechete, ine ndikufuna inu mumupatse Iye mathokozo ndi matamando. Munene, “Ambuye, ine ndikukuthokozani Inu kwambiri poyeretsa solo yanga. Ine ndikukuthokozani inu chifukwa cha zonse zimene Inu mwandichitira ine. Mulole Mzimu Wanu ukhale pa ine kudutsa tsikuli, Ambuye. Nditsogoleleni ine. Ndilondolereni ine. Ndidalitseni ine.” Mulungu apereke mdalitso umenewo kwa inu, ndiro pemphero langa.

Tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu, M'bale Neville, inu mutibalalitse ife mu mawu a pemphero. 

MIZIMU YODOLOLA CHA55-0724
(Enticing Spirits)

MAULIKI A PHUNZIRO LA ZIWANDA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Julaye 24, 1955, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org